# Buku la Mphunzitsi

Nthawiyabaibulo
Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri

Maphunziro C1 - C6

www.besweb.com

## Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

**Cholinga cha Utumiki**
Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

**Masomphenya a Utumiki**
Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

## ZOYENERA KUDZIWA

**Zomwe a Bible Educational Services amachita**
A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a "Nthawiyabaibulo", "Moyo Watsopano" ndi "Okolola" a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – www.besweb.com kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

## Keyala

**International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)**
Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA
Phone: 00 44 286 632 2462
Email: sam@besweb.com

**UK Secretary – Editorial feedback**
Mr Stephen Gillham
Email: stephen.gillham@besweb.com

**Web address:** www.besweb.com
**Email address:** info@besweb.com

## BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

## KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayesetse kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera tayesetsa kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: ***ITALICS***.
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira kotero kuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheka yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku www.freebibleimages.org (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

## Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M'buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.

    1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
    2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
    3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
    4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

"Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa."

## Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

| | KALASI 0 (sanayambe sukulu)<br>Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7)<br>Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10) | Kalasi Yachitatu<br>(Zaka 11-13) | Kalasi Yachinayi<br>(Zaka 14+) |
|---|---|---|---|
| MAPHUNZIRO A | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Abrahamu<br>6. Abrahamu<br>7. Petro<br>8. Petro<br>9. Yakobo<br>10. Akhristu Oyambirira<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Pemphero<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe ndi Kugwa<br>2. Zochitika Zoyamba - Genesis<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Moyo wa Chikhristu<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO B | 1. Moyo Woyambirira wa Khristu<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Mafanizo<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Alembi a Uthenga Wabwino<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yakobo ndi Banja Lake<br>7. Yosefe<br>8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Lamulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO C | 1. Danieli<br>2. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>3. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute ndi Samueli<br>6. Davide<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Yona<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>3. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Zoyankhula za Yesu<br>3. Mphamvu za Ambuye<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |

## C1 Nkhani Yoyamba

**Danieli – Dziko lachilendo – Iyi ndi nkhani ya kukondweretsa Mulungu ponena "ayi" pa zinthu zolakwika.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Mulungu anathandiza Danieli ndi anzake chifukwa cha kukhulupirika pamaso pake.<br>• Tikuyenera kukhala okhulupirika kwa Mulungu ngakhale zinthu zikuvuta.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Danieli 1: 20***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Danieli 1: 1-21*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kalasi ya Brenda inkalemba mayeso. Mafunso anali ovuta. M'phunzitsi anayika ophunzira onse motalikana kuti asathe kuwonerana. Koma Brenda ankatha kuona mayankho amene Teresa ankalemba. Teresa nthawi zonse ankakhoza. Brenda anaganiza zoti aonere ndi kulemba zomwe Teresa walemba poganiza kuti aphunzitsi sadziwa. Iye adzakhoza bwino ndipo amayi ake akakondwera. Koma Mulungu akanakondwera? Brenda ankadziwa kuti kunali kofunika kuti wina asabe mayankho a munthu wina. Iye anakumbukira lamulo limodzi la Mulungu loti usabe. Choncho m'malo muwonera, Brenda anaganiza kwambiri ndi kuyesetsa kuyankha mafunso ovuta aja. Pamapeto pake Brenda anazindikira kuti anakhoza. Kuchita chinthu choyenera ndi kwabwino kwambiri! M'phunziro la lero, Danieli ndi anzake anayenera kusankha pakati pa kuchita choyenera chomwe chimakondweretsa Mulungu kapena kuchita chinthu chimene chichititsa moyo wawo kukhala osavuta. |
| **PHUNZITSANI** | • Danieli ndi anzake atatu aja anali Ahebri (anthu osankhidwa ndi Mulungu) ndipo ankakhala mu Yerusalemu. Tsiku lina mdani wawo mfumu Nebukadinezara anadzathira nkhondo mzinda wawo ndi kuwagwira pamodzi ndi anthu ena. Iwo anapita ku dziko la kutali ku Babulo kumene anakalowa mu sukulu yapadera ndi kuphunzira chiyankhulo chatsopano cha dziko latsopanolo. *Afunseni ana kuti afotokoze kuti zinthu zinali zotani kwa iwo.* ***(Danieli 1: 1-4)***<br>• Danieli ndi anzake anapatsidwa mayina atsopano a Chibabulo *(Onani izi mu Kalasi 2)* ndi chakudya kuchokera pa tebulo ya mfumu. Mfumu inkafuna kuti akhale amphamvu kuti azitha kumutumikira m'nyumba yake yaufumu. Mfumu Nebukadinezara inafuna kuti Danieli ndi anzake ayiwale zonse za ku dziko lawo komanso Mulungu m'modzi yekha owona amene iwo ankatumikira. ***(Danieli 1: 5-7)***<br>• *Kambiranani za kuyipa kwa zimenezi.*<br>• Danieli ndi anzake ankakonda Mulungu ndipo anafuna kumumvera ngakhale anali m'dziko lachilendo kumene anthu ankatsatira milungu ina. Iwo ankadziwa kuti sankayenera kudya chakudya cha mfumu chifukwa chinali chitaperekedwa ku milungu yabodza. *Kodi iwo akanachita chiyani?* Iwo anatsimikiza za kuti sadzadya chakudya cha mfumu ngakhale kuti mfumuyo idzakwiya nazo. *Kambiranani tanthauzo la kukhulupirika pamaso pa Mulungu. Ife nthawi zonse tikuyenera kuchita zimene Mulungu amanena ngakhale zitaoneka kuti ndi zovuta ndiponso kuti anthu ena akufuna tichite zinthu zina zosiyana.*<br>• Pamene iwo anawuza othandiza mfumu zimene ankafuna kuchita, othandizawo anadandaula!<br>• Kodi zikanatha bwanji ngati Danieli ndi anzake aja sakanaoneka amphamvu ndi athanzi monga anzawo ena pa sukulu ya mfumuyo? ***(Danieli 1: 8-10)*** Danieli anakhulupirira kuti Mulungu adzamusamalira.<br>• Iye anapempha othandiza mfumu aja kuti aziwapatsa ndiwo za masamba ndi madzi kwa masiku khumi. Nthawiyo itakwana othandiza a mfumu anadabwa kuona Danieli ndi anzake aja ali athanzi ndi amphamvu kuposa anthu amene ankadya chakudya cha mfumu. ***(Danieli 1: 11-15)*** *Kodi mukuganiza kuti ichi chinali chifukwa chiyani?*<br>• Kuyambira nthawi imeneyo Danieli ndi anzake aja ankapatsidwa ndiwo za masamba ndi madzi basi. Mulungu anali ndi Danieli ndi anzake aja ndipo anawadalitsa chifukwa cha kukhulupirika kwawo. Iye anawapatsa nzeru ndiponso kuthandiza Danieli kumasulira maloto. ***(Danieli 1: 16-17)*** *Fotokozani kuti Danieli ndi anzake sanali ndi chakudya chabwino chokha, komanso anali ndi Mulungu.*<br>• Patatha zaka zitatu, achinyamata onse anabwera nawo pamaso pa mfumu. Pakati pa anthu onsewo, mfumu inapeza kuti Danieli ndi anzake aja anali abwino kwambiri. Iye anawaona kuti anali anzeru kwambiri kuposa alangizi ena onse amene anali nawo. *Tsindikani kuti iwo anatenga Mulungu kukhala woyamba ngakhale analangidwa chifukwa cha kusamvera lamulo la mfumu.* ***(Danieli 1: 18-21)***<br>• *Akhristu amakhulupirira kuti n'kofunika kunena kuti 'inde' pa zimene Mulungu akunena ndi kukhala okhulupirika kwa Iye.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI mu Zoonjezera A – Dziko lachilendo. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Danieli 1: 20.***<br>Ana a Kalasi 1 aphunzire gawo lachiwiri la vesili. |
| **KUMBUKIRANI** | **Kalasi 1** - Kalasi lijambule zakudya za masamba ndi kuziyika m'gulu la maphunziro a Zakudya Zopatsa Thanzi. Gwiritsani ntchito mapepala a mitundu yosiyanasiyana, nsalu ndi zina.<br>**Kalasi 2** – Kukhala m'magulu, ana achite sewero la nkhani imeneyi. Sankhani anthu a mu nkhaniyi amene mukufuna anawo aonetse ndipo athandize m'mene zinachitikira. |

**C1 Nkhani Yachiwiri**

**Fano la Nebukadinezara– Iyi ndi nkhani ya anzake a Danieli kunena "ayi" pa zimene ndi zolakwika.**

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Sadrake, Mesake ndi Abedinego anakhulupirira ndi kumvera Mulungu.
- Ife titha kukhulupirira Mulungu kuti adzakhala nafe pamene tikudutsa m'mayesero.

**Vesi Yoloweza:** ***Danieli 3: 17***

**Ndime Yowerenga:** ***Danieli 2: 48-49 ndi 3: 1-30***

**MAWU OYAMBA**

Nebukadinezara sankakhulupirira za kupembedza Mulungu m'modzi ndi owona yekha. Iye ankapembedza mafano kapena milungu yopangidwa ndi zitsulo kapena mwala, koma izi sizinali zoyenera chifukwa zinalibe mphamvu yothandiza wina aliyense. Danieli ndi anzake atatu aja ankadziwa kuti kunali kulakwa kupembedza mafano chifukwa Mulungu ananena mu lamulo lachiwiri - ***Eksodo 20: 4***.

**PHUNZITSANI**

- Anzake atatu a Danieli, Sadrake, Mesake ndi Abedinego, anali Ahebri amene ankakhulupirira Mulungu m'modzi ndi owona ndipo ankafuna kumvera Iye. *(Kumbutsani ana zochitika mu Nkhani Yoyamba.)* Iwo sakanapembedza mafano. Mulungu anawathandiza kuti akhale anthu ofunika kwambiri ku Babulo. ***(Danieli 2: 48-49)***
- Mfumu Nebukadinezara inapanga fano la golide. Linali lotalika mamita 27 ndipo mulifupi mwake munali mamita atatu. (Kufanana ndi galimoto 24 zosanjikana.) Iye analamula kuti anthu ake onse ofunika mu ufumu wake, kuphatikizapo Sadrake, Mesake ndi Abedinego, abwere ku mwambo wapadera. Mfumu inalamula kuti akamva kulira kwa zida zoyimbira, aliyense agwade ndi kupembedza fano la golide. Aliyense amene sagwada adzaponyedwa m'ng'anjo yamoto. *Fotokozani kuti ng'anjo yamoto ndi chiyani.* ***(Danieli 3: 1-6)***
- Pamene anamva kulira kwa zida zoyimbira, anthu anagwada ndi kupembedza fanolo. Onse anagwada kupatula Sadrake, Mesake ndi Abedinego. *Chifukwa chiyani? Iwo ankadziwa Mawu a Mulungu amene analamula kuti anthu ake asagwadire mafano.* Sadrake, Mesake ndi Abedinego anakana kusamvera Mulungu ngakhale kuti kutero kukanachititsa kuti aponyedwe m'moto. ***(Daniel 3: 7)***
- Nduna zina zinakawuza mfumu kuti Sadrake, Mesake ndi Abedinego sanagwadire fanolo. Mfumu inakwiya kwambiri! Iyo inawawuza kuti akuyenera kugwada ndi kupembedza koma akakana adzaponyedwa m'ng'anjo yamoto. Mfumu inawawuza kuti panalibe mulungu wamphamvu amene akanatha kuwapulumutsa. ***(Danieli 3: 8-15)***. *Funsani ana kuti akuwuzeni amene akuganiza kuti ndi wamphamvu atha kupulumutsa anthu.*
- Anthu atatuwa anayankha kuti, "Ngati tiponyedwa m'ng'anjo yamoto, Mulungu amene timamutumikira akhoza kutipulumutsa" *(Vesi Yoloweza)*. Mfumu Nebukadinezara inalamula kuti ayitenthetsa ng'anjo kasanu ndi kawiri. Anthu atatuwa anaponyedwa m'ng'anjo yamoto. ***(Danieli 3: 16-23)***
- Kenaka mfumu inadabwa kwambiri. Iye analamula kuti anthu atatu aponyedwe m'moto koma tsopano akuona anayi! Iwo ankayendayenda m'moto osapsamo. Iye anaganiza kuti munthu wachinayiyo ankaoneka ngati 'mwana wa milungu'. ***(Danieli 3: 24-25)***
- Mfumu Nebukadinezara inalamula kuti atuluke m'moto. Anthuwo sanapwetekedwe m'pang'ono pomwe. Nebukadinezara anatamanda Mulungu ponena kuti Iye wawapulumutsa chifukwa anamukhulupirira ndi kumumvera. Iye anadziwa kuti panalibe mulungu wina aliyense akanapulumutsa anthu ake m'njira imeneyi. Iye anapereka kwa atatu onsewa maudindo apamwamba mu ufumu wake. ***(Danieli 3: 26-30)***
- *Fotokozani kuti Mulungu amafuna ife kuti tizimumvera ndi kumudalira kwathunthu. Izi zikutanthauza kuti tikuyenera kudziwa Mawu ake ndi kumvetsetsa malamulo ake. Iye analonjeza kuti adzakhala nafe m'masautso athu onse. Iye akhoza kutipulumutsa!* ***Werengani Yesaya 43: 2***.

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**

**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Fano la Nebukadinezara.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza imene ndi gawo la nkhaniyi: ***Danieli 3: 17***. Tsindikani pa - "Mulungu amene timamutumikira akhoza kutipulumutsa."

**KUMBUKIRANI**

Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:

- Kodi anthu atatu amene ali mu nkhani yathu anapatsidwa mayina anji?
- Kodi mfumu dzina lake linali ndani?
- Kodi Mfumu Nebukadinezara inapanga chiyani?
- Kodi tikudziwa bwanji kuti Mulungu sankakondwera ndi fano limeneli?
- Kodi chikanachitika ndi chiyani kwa anthu amene sakanagwadira fano?
- Anthu atatu anasankha kumvera Mulungu. 'Kumvera' ndi chiyani?
- Mfumu inachita chiyani itaona kuti atetezedwa?

## C1 Nkhani Yachitatu

**Danieli – Zenera lotsekula – Iyi ndi nkhani ya kuoona mtima kwa Danieli ndi kupemphera kwake kwa Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Nsanje ya adani a Danieli inali yolakwika.<br>• Ngati ife tikonda Ambuye monga Danieli, tidzakhala owona mtima ndi odalirika.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Danieli 6: 16***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Danieli 6: 1-16*** |
| **MAWU OYAMBA** | **Kalasi 1** - Yankhulani za kulira kwa nyama zosiyanasiyana. Chitani sewero lomwe ana alira ngati nyama ndipo ena azitchula nyama yake. Potsiriza khazikikani pa kubangula kwa mkango. Lolani ana abangule ngati mkango ndipo muwawuze kuti mkango wa mu nkhani ya lero unali wotero, 'Rrrrr!!'<br>**Kalasi 2** - Yankhulani za nsanje. Kodi munachitapo nsanje chifukwa mnzanu wina anasankhidwa koma osati inu? Mwina nsanjeyo inali yayikulu ndipo munkafuna kuti choyipa chimuchitikire munthuyo. Izi ndiye zinachitika mu nkhani yathu ya lero. Fotokozani kuti nsanje ndi tchimo ndipo imabweretsa udani. |
| **PHUNZITSANI** | • Ku Babulo kunali mfumu yatsopano yotchedwa Dariyo. Panali nduna zazikulu zitatu ndipo Danieli anali m'modzi mwa iwo! Danieli ankagwira ntchito molimbikika ndiponso ankagwira ntchito bwino kwambiri. Mfumu Dariyo anafuna kumuyika iye kukhale woyang'anira nduna zinzakezo. ***(Danieli 6: 1-3)***<br>• Pamene enawo anamva izi anamuchitira nsanje Danieli. Iwo sankafuna kuti iye aziwalamulira. Iwo anayesetsa kupeza cholakwika kuti akawuze mfumu kuti asamakondenso Danieli ndi kusintha maganizo ake omupatsa udindo wofunika kwambiri. Mwachitsanzo, kodi Danieli ananenapo zabodza kwa mfumu kapena kuba china chilichonse? Iwo anaganiza kwambiri koma sanathe kupeza chilichonse chomwe akanatha kukawuza Mfumu Dariyo. Iwo ankadziwa kuti Danieli anali munthu woona mtima ndi wodalirika. ***(Danieli 6: 4)*** *Pamene munthu ali wodalirika zikutanthauza kuti anthu ena angathe kuwadalira kuti achita zomwe anena kuti achitezo. Fotokozani kuti izi ndi zimene Mulungu amafuna kuti otsatira ake akhale.*<br>• Adani a Danieli anapeza njira yatsopano yoti aonetsa kuti Danieli ndi munthu woyipa. Iwo ankadziwa kuti nthawi zambiri ankapemphera kwa Mulungu. Iwo anaganiza zomupezera cholakwa Danieli. Iwo anapita kwa Mfumu Dariyo ndi kumupempha kuti apange lamulo latsopano lonena kuti kwa masiku makumi atatu munthu aliyense azipemphera kwa mfumu yokha. Ngati munthu apemphera kwa wina aliyense, adzaponyedwa m'dzenje la mikango. Mfumu inavomera ndipo inavomereza lamulo latsopano. ***(Danieli 6: 5-9)***<br>• Danieli anamva za lamulo latsopanoli. Iye ankadziwa kuti linali lofuna kumupezera cholakwa koma iye anadalira Mulungu kuti adzamuteteza. Pemphero linali lofunika kwambiri kwa iye ndipo ngakhale ankadziwa kuti zinali zovuta kwambiri kutero, iye analowa m'chipinda mwake ndi kumapemphera katatu pa tsiku monga m'mene ankachitira nthawi zonse. *Khalani ndi nthawi yoti mukambirane kuti pemphero ndi chiyani ndi kufunika kwake pa moyo wa Mkhristu.* Pamene Danieli ankapemphera, adani ake anamuona. Iwo anapita kukawuza mfumu zomwe Danieli ankachita. ***(Danieli 6: 10-13)***<br>• Mfumu inakwiya kwambiri! Iyo sinafune kuponya Danieli m'dzenje la mikango koma lamulo lomwe inakhazikitsa sikanatha kulisintha. Iyo palibe chomwe ikanachita kuti ithandize Danieli. Mfumu inalamula kuti akatenge Danieli ndi kumuponya m'dzenje la mikango. Mfumu inawuza Danieli kuti Mulungu amene amamutumukira nthawi zonse adzamupulumutsa. ***(Danieli 6: 14-16)*** *Kambirananani ndi ana zomwe akuganiza kuti kenaka zinachitika. Ndani amene angathe kupulumutsa Danieli?*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Zenera lotsekula. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Danieli 6: 16***. |
| **KUMBUKIRANI** | Lembani mawu awa pa khoma kapena pa pepala. Funsani ana kuti asankhe makhalidwe abwino pakati pa makhalidwe oyipa.<br>kuwona mtima nsanje kugwira ntchito molimbika kudalirika kunena nthano<br>kufuna zomwe ena ali nazo chidani kupemphera kunena zoona<br><br>Kumbutsani ana kuti Mulungu angathe kugwira ntchito mwa ife ndi cholinga chakuti miyoyo yathu ikondweretse Iye. |

## C1 Nkhani Yachinayi

**Danieli - Dzenje la mikango – Iyi ndi nkhani ya kudalira Mulungu nthawi zonse.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Danieli anatumikira Mulungu mokhulupirika.<br>• Mulungu ndi Mulungu amene amalanditsa ndi kupulumutsa.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Danieli 6: 22***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Danieli 6: 17-28*** |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana kuti akhale awiriawiri kuti akambirane nkhani ya phunziro latha. Kodi iwo angapereke mayankho a mafunso awa?<br>Kodi Danieli ankagwira bwino ntchito yake? Kodi mfumu Dariyo inkafuna kuchita chiyani kwa Danieli? Kodi n'chifukwa chiyani adani a Danieli anali ndi nsanje? N'chifukwa chiyani anaponya Danieli m'dzenje la mikango? Kodi Mfumu Dariyo inkafuna kuti Danieli aponyedwe m'dzenje la mikango?<br>Funsani ana awiriawiri kuti akupatseni mayankho. *Kenaka kambiranani ndi ana zomwe akuganiza kuti kenaka zinachitika. Kumbutsani ana kuti Danieli anadalira Mulungu ngakhale mu nthawi yoopsa ngati imeneyi. Kodi angakumbukire zitsanzo zofanana ndi iyi kuchokera mu nkhani yoyamba ndi yachiwiri?* |
| **PHUNZITSANI** | • Danieli anaponyedwa m'dzenje la mikango. Mfumu inati kwa iye, "Mulungu wako amene umutumikira nthawi zonse, akupulumutse." Anatseka ndi mwala pa khomo la dzenje ndi kumata. Mfumu inapita ku nyumba yake yaufumu. Mfumu sinadye chilichonse ndipo sinagone. Mfumu inkaganizira za kukhulupirika ndi kudalirika kwa wantchito wake, Danieli. ***(Danieli 6: 16-18)***<br>• M'mamawa, tsiku lotsatira, mfumu inanyamuka kupita ku dzenje la mikango. Mfumu inayitana Danieli ndi kufunsa ngati Mulungu wake anamupulumutsa kwa mikango. Mfumu inasangalala kwambiri pamene inamva mawu a Danieli. Danieli anayankha ponena kuti Mulungu anatumiza mngelo amene anatseka pakamwa pa mikango kuti isamudye. Mulungu ankadziwa kuti Danieli sanachite cholakwa chilichonse; n'chifukwa chake anamuteteza. *Kambiranani momwe mfumu inkamvera mu mtima mwake tsopano.* Mfumu Dariyo inalamula kuti amutulutse Danieli m'dzenje la mikango. Mfumu inalamula kuti anthu oyipa aja amene ananena zoyipa za Danieli aponyedwe m'dzenje la mikango. ***(Danieli 6: 19-24)***<br>• Mfumu Dariyo inalembera anthu onse amene ankakhala mu ufumu wake. Inalamula kuti onse akhulupirire Mulungu wamoyo ndi kuwawuza momwe Mulungu anapulumutsira Danieli m'dzenje la mikango. Mfumu inawawuza kuti Mulungu ndi Mulungu amene amapulumutsa ndi kulanditsa. ***(Danieli 6: 25-28)***<br>• *Mulungu atha kutipulumutsa ife ku chilango cha machimo athu. Ambuye Yesu anafa pa mtanda, kulangidwa chifukwa cha machimo athu. Ngati tikhulupirira kuti anafa chifukwa cha ife, Mulungu adzatikhululukira ndi kutipatsa moyo wosatha.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Dzenje la mikango. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Danieli 6: 22***. Ana aphunzire gawo loyamba la vesi. |
| **KUMBUKIRANI** | **Kalasi 1** – Ngati mumadziwa nyimbo za Danieli, ana aziphunzire.<br>**Kalasi 2** - M'phunzitsi kapena mwana akhale ngati Danieli. Ana afunse 'Danieli' mafunso a zomwe zinachitika ndi momwe ankamva mu mtima mwake. |

## C2 Nkhani Yoyamba

**Munthu wosaona aona – Iyi ndi nkhani ya Yesu kuthandiza munthu amene anakhulupirira Iye.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu ndi Mulungu ndipo angathe kuchita zinthu zodabwitsa.<br>• Yesu amamva tikamuyitana.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 18: 43***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 18: 35-43 (Marko 10:46-52-Kalasi 0 ndi 1)*** |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana kuti atsinzine ndi kukhala ngati ndi osaona. Kodi akuona bwanji ngati atakhala otero? Fotokozerani ana kuti mu nthawi ya Yesu munthu wosaona analibe thandizo, koma kupempha kuti akhale ndi moyo. Palibe amene ankasamalira anthu osaona. Koma mu nkhani yathu ya lero, tidzamva za chisamaliro cha Yesu kwa munthu wosaona. |
| **PHUNZITSANI** | • Yesu ankapita ku Yerusalemu pamodzi ndi ophunzira ake. (Kalasi 2 – Mufotokoze kuti ankapita kumeneko kukagwira ntchito imene Atate anamutuma kuti agwire pakufa pa mtanda.)<br>• Ali pa ulendo anafika mu mzinda wa Yeriko.<br>• *Yankhulani za kusonkhana kwa anthu munthu wofunika akamabwera.*<br>• Gulu la anthu linasonkhana kuti lione Yesu pamene akulowa mu Yeriko. *N'chifukwa chiyani ankafuna kumuona?*<br>• M'mbali mwa msewu munali munthu wosaona amene ankapempha pa malo ake nthawi zonse. Koma tsiku limenelo anadziwa kuti chinthu china chikuchitika! *Funsani ana kuti afotokoze m'mene anadziwira kuti china chake chikuchitika - kuyenda kwa anthu, phokoso, chisangalalo, kufunsa wina ndi kuwuzidwa kuti Yesu wa ku Nazarete akudutsa.* ***(Luka 18: 35-37)***<br>• *Fotokozani za chisangalalo cha munthuyu ndi kuti sakanatha kukhala chete pamene anamva kuti anali Yesu.* Iye sankamuona Yesu koma anamuyitana ndi mawu ofuwula! Awuze momwe anayitanira Yesu "Yesu, Mwana wa Davide, mundichitire chifundo ine." Izi zikuonetsa kuti anazindikira chimene Yesu anali - wotumidwa ndi Mulungu – ndiponso anadziwa kuti Yesu angathe kumuthandiza m'njira imene wina aliyense sakanatha. ***(Luka 18: 38)***<br>• Anthu ena anayesa kumuletsa. *Funsani ana kuti ayesere kupeza chifukwa chake. Yankhulani kuti Yesu ali ndi nthawi yoyankhulana ndi wina aliyense ndi kuti ali ndi chidwi ndi aliyense wa ife.* Munthuyu anatsimikiza ndipo anapitirira kuyitana Yesu. Yesu anamva ndipo anawuza anthu kuti abwere naye kwa Iye. ***(Luka 18: 39-40)***<br>• Ndipo Yesu anayankhulana ndi munthuyo – ***werengani vesi 41***. Pamene munthuyo ananena kuti akufuna kuti ayambe kuona, ankaonetsa kuti ankakhulupirira kuti Yesu angathe kuchita zimenezi kwa iye. Yesu anakondwera kuti munthuyu anamudalira ndi kuonetsa chikhulupiriro pa Iye. *Fotokozani momwe Yesu anachitira pochiza kusaona ponena kuti, "Landira kuona kwako." Mawu a Yesu anali amphamvu. Palibe wina aliyense akanatha kuchita zimenezi.* ***(Luka 18:41-42)***<br>• *Funsani ana zomwe munthuyo anayamba kuona ndi zomwe ankamva mu mtima mwake pamene Yesu anamupatsa kuona. Nanga gulu la anthu linachita chiyani? Tsimikizirani mayankho a ana powerenga zomwe Baibulo likunena.* ***(Luka 18: 43)***<br>• *Yesu akufuna kuthandiza anthu ndi kuwachitira zabwino. Pamene tikuyenda tokha zili ngati kuyenda mu mdima. Kumbutsani ana kuti Yesu ndi Kuunika kwa Dziko Lapansi ndipo pamene tikumutsata, timayenda mu njira yoyenera ya kuunika.* ***(Yohane 8: 12)***<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Munthu wosaona aona. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Luka 18: 43***. |
| **KUMBUKIRANI** | Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:<br>• Kodi Yesu ankafika mu mzinda uti?<br>• Kodi Yesu anali ndi ndani?<br>• Kodi ndi ndani ankakhala kunja kwa mzinda?<br>• N'chifukwa chiyani munthuyo ankapempha?<br>• Kodi munthuyo anati Yesu ndi ndani?<br>• Kodi munthuyo ankafuna Yesu achite chiyani?<br>• Kodi munthuyo anachita chiyani atachiritsidwa ndi Yesu?<br>• Kodi gulu la anthu linachita chiyani? |

## C2 Nkhani Yachiwiri

**Kudyetsa gulu la anthu – Iyi ndi nkhani ya Yesu kudyetsa anthu anjala.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Ndi Yesu yekha amene angakwaniritse zosowa za anthu anjala.
- Yesu ndi Mkate Wamoyo ndipo amapereka moyo wosatha.

**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 6: 35***
**Ndime Yowerenga:** ***Yohane 6: 1-14***

### MAWU OYAMBA

**Kalasi 1** - Yerekezani ngati mwapita ndi ana kutali. Kumeneko kukhala ndani, muzidya chiyani ndipo muzidyera kuti?
**Kalasi 2** - Yankhulani za kupita kukamvera kapena kukaona munthu wina wapadera akuyankhula, kuyimba, kuchita masewero ndi zina zambiri. Munthuyo atha kukhala wotchuka, koma pakapita nthawi inu mudzamva chiyani mu mtima mwanu? Mwina mudzamva kutopa, kuyipidwa, kutentha ndi kusowa mtendere. Yesu ankafuna kuonetsa gulu la anthu ndi ophunzira ake kuti amatha kukwaniritsa zosowa zawo zonse.

### PHUNZITSANI

- Yesu ankafuna kukhala ndi nthawi ndi ophunzira ake kuti awaphunzitse zinthu zofunika kwambiri za Mulungu. *Fotokozani za kumene anali – kumalo opanda anthu ku phiri.* Koma ngakhale kumeneko, anthu ena anabwera ndi kudzawapeza. *Funsani ana kuti aganizire chifukwa chimene anthu anabwera kudzafuna Yesu.* Pasanapite nthawi, gulu lalikulu linasonkhana. ***(Yohane 6: 1-3)***
- *Kodi Yesu anamva bwanji mu mtima pamene ena anabwera kudzakhala naye?* Fotokozani kuti Yesu sanafune zowabweza anthu amenewa. Iwo analinso ofunika kwambiri kwa Iye ndipo anawachitira chifundo. ***(Mateyu 14: 14)***
- Iye anafunsa Filipo, m'modzi mwa ophunzira, funso, "Kodi tingagule kuti buledi kuti anthu awa adye?" Fotokozani kuti Yesu ankafuna kumuyesa Filipo kuti adziwe ngati ankakhulupirira kuti Yesu angathandize. *Kodi anawo akanayankha kuti chiyani?* Filipo sanathe kuona momwe akanakonzera vuto limenelo; iye anafotokoza pankafunika ndalama za malipiro a chaka chimodzi a munthu kuti aliyense wa anthuwo adye. ***(Yohane 6: 5-7)***
- Andreya anapeza mnyamata amene anali ndi chakudya chake ndipo anabwera nacho kwa Yesu.
- *Kwa ana a Kalasi 1 khalani ndi kabokosi ka chakudya ndipo atsekule kuti aone timalofu tisanu ndi tinsomba tiwiri.* Monga Filipo, Andreya ankadziwa kuti izi sizinali zokwanira.
- *Funsani ana kuti aganize za munthu amene angathe kupereka chakudya kwa gulu lalikulu la anthu. Pitirizani kufotokoza momwe Yesu anakwaniritsira chosowa cha aliyense ponena mfundo zotsatira.* ***(Yohane 6: 8-9)***
- Iye anawuza ophunzira kuti awuze anthu kuti akhale pansi.
- Iye anayamika Mulungu chifukwa cha chakudya. *(Zochita – n'kofunika kwa ife kukumbukira kuti chakudya chathu chimachokera kwa Mulungu.)*
- Iye anagawa chakudyacho, anachipereka ndipo chinakwanirira aliyense.
- Palibe chimene chinaonongeka – chinatsala chokwana madengu khumi ndi awiri. *(Zochita – tisamaononge chakudya.)*
- *Onetsani kudabwa kuti chinali chokwanira aliyense – gulu la anthu oposa 5000! Fotokozani kuti ana amvetse kuchuluka kwa anthuwa.* Anthu anayamba kuganiza kuti Yesu anali Mesiya wolonjezedwa wochokera kwa Mulungu chifukwa anali asanaone chinthu ngati chimenechi n'kale lomwe. ***(Yohane 6: 10-14)***
- Pambuyo pake, Yesu anayankhula ndi ophunzira ake zomwe zinachitikazo. Iye anawawuza za kuti Iye ndi "Mkate Wamoyo." Yesu anathetsa njala ya anthu koma akanatha kuchita zoposa izi. Iye ndi Wopereka moyo wosatha .... kutanthauza kuti Iye atha kutipatsa moyo wabwino kwambiri umene udzatilowetsa m'banja la Mulungu. ***(Yohane 6: 35)***

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**
**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kudyetsa gulu la anthu.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Yohane 6: 35***.

### KUMBUKIRANI

Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:
- Kodi Yesu ndi ophunzira ake anali kuti?
- N'chifukwa chiyani anthu ambiri ankafuna kuona Yesu?
- Kodi Filipo anati chiyani pamene Yesu anafunsa kuti akagule zakudya?
- Kodi mnyamata uja anali ndi chakudya chiti?
- Kod Yesu anadyetsa anthu angati?
- Kodi anatsala ndi madengu angati?
- Kodi Yesu anawuza ophunzira ake kuti Iye anali ndani?
- Kodi dzinali likutiphunzitsa kuti ndi chiyani chimene Yesu amapereka?

## C2 Nkhani Yachitatu

**Munthu wolumala ayenda – Iyi ndi nkhani ya Yesu kuchiritsa munthu amene sankatha kuyenda.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu ali ndi mphamvu zochititsa munthu kuyenda.<br>• Ndi Yesu yekha amene amatha kukhululukira machimo.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 5: 24***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yohane 5: 1-15*** |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana kuti afotokoze zomwe zinachitika atathyoka mwendo kapena atavulala. Yankhulani momwe zimachitikira mukamadalira ena m'malo mochita zinthu nokha. Kodi chiyani chimene anali nacho chowathandiza kuyenda, monga ndodo kapena njinga yokhalapo? Lingalirani za nkhani ya lero – zaka 38 munthu sakutha kuyenda komanso popanda abale oti n'kumuthandiza! Ana m'kalasi atchule mabungwe amene amachita zachifundo zothandiza anthu olumala ndiponso apeze njira zowathandizira. Nthawi zonse muzisamala zinthu zimene ana akukumana nazo m'mabanja awo. |
| **PHUNZITSANI** | • **Yesu pa Dziwe -** Yesu anali mu Yerusalemu pa phwando lapadera. ***(Yohane 5: 1)***<br>• Mu Yerusalemu munali dziwe ndipo anthu ankakhulupirira kuti pamene madzi akuvundulidwa, munthu woyamba kulowamo ankachiritsidwa. Anthu ambiri osaona, olumala ndi ofa ziwalo ankakhala mozungulira dziwelo.<br>• *Kambiranani zomwe anthuwa ankamva m'mitima mwawo, chitsanzo: chiyembekezo, chisangalalo, nkhawa, kukhumudwa, kutaya mtima...* Yesu anafika pa dziwepo ndi kuzindikira kuti munthu wolumala anali atakhala pamenepo zaka 38. *(Onetsetsani kuti ana akudziwa kuti munthu wolumalayu sankatha kuyenda.)* Yesu anapita kukamufunsa ngati ankafuna kuchira.<br>• Munthu wolumayo anafotokoza kuti ankalephera kulowa m'madzi chifukwa analibe womuthandiza. *Werengani kukambirana kwawo pa* ***vesi 7 ndi 8***. Munthu analibe wina aliyense woti akanamuthandiza. ***(Yohane 5: 5-8)***<br>• *Tsindikani kuti Yesu ankawuza munthuyu kuti achite chinthu sankatha kuchita kwa zaka 38!* Pamene Yesu ankamuwuza kuti ayimirire, munthuyo anapatsidwa mphamvu zoti athe kuyenda. Munthu anachiritsidwa nthawi yomweyo, anayimira ndi kunyamula mphasa yake kuyamba kuyenda. ***(Yohane 5: 8-9)***<br>• **Ayuda akupeza cholakwa -** *Fotokozani kuti munthuyo anachiritsidwa tsiku la Sabata (loweruka). Ayuda anali ndi malamulo ambiri oletsa zomwe munthu sankayenera kuchita tsiku limeneli.* Iwo anaona kuti munthuyo walakwa ponyamula mphasa yake. Munthuyo anati amene anamuchiritsa ndi amene anamuwuza kuti achite izi, ndipo anavomereza kuti sankamudziwa munthuyo. ***(Yohane 5: 10-12)***<br>• **Yesu m'Nyumba ya Mulungu -** ***(Yohane 5: 14-15)*** Pambuyo pake, Yesu anamuona munthuyo ali m'Nyumba ya Mulungu ndipo anayankhula naye, kumuwuza kuti asiye kuchimwa. *Fotokozani kuti "kuchimwa" ndi chiyani* – tonse timachimwira Mulungu kudzera mu zimene timaganiza, kuyankhula ndi kuchita. Munthu anali ndi zosowa za mitundu iwiri, kufuna kuti ayende ndi kukhululukidwa tchimo lake. Iye sanamuzindikire Yesu pamene thupi lake linachiritsidwa koma tsopano anapatsidwa mwayi woti aphunzire zambiri za chimene Yesu anali ndi zomwe akanamuchitira.<br>• *Fotokozani kuti ndi Ambuye Yesu wokha amene amakhululukira machimo. Tikuyenera kukhululukidwa machimo athu kuti miyoyo yathu ikhale pa ubale wabwino ndi Mulungu ndi kuyamba kumutumikira.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Munthu wolumala ayenda. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani Vesi Yoloweza yomwe ndi mbali imodzi ya nkhaniyi: ***Yohane 5: 24***. |
| **KUMBUKIRANI** | Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:<br>• Kodi Yesu anali mu mzinda uti?<br>• N'chifukwa chiyani ambiri odwala ndi ovulala ankakhala pa dziweli?<br>• N'chifukwa chiyani munthuyu anakhala pamenepa nthawi yayitali?<br>• Kodi Yesu anawuza munthuyu kuti achite chiyani?<br>• N'chifukwa chiyani Ayuda anayipidwa ndi munthuyu?<br>• Kodi Yesu anamuonanso munthuyu kuti?<br>• Kodi nthawi imeneyi anawuza munthuyu kuti achite chiyani?<br>• N'chifukwa chiyani sanamvetsetse za Yesu? |

**C2 Nkhani Yachinayi**

**Mtsikana womwalira akhala moyo! – Iyi ndi nkhani ya Yesu kupereka moyo watsopano.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu amathandiza amene amabwera kwa Iye.<br>• Palibe chinthu chimene Yesu sangathe kuchita.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Marko 5: 42***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Marko 5: 21-43*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za anthu olemekezeka a kumene mumakhala – chitsanzo, ana atchule ntchito zimene anthuwo amagwira kapena udindo wawo m'boma, m'bwalo la milandu, ku polisi ndi malo ena ambiri. Nkhani yathu lero ndi munthu wolemekezeka amene ankafuna thandizo. Kupempha thandizo sikophweka nthawi zambiri, makamaka ngati ndiwe munthu wa ulemu wake. |
| **PHUNZITSANI** | • Ambuye Yesu apa analinso ndi gulu la anthu lomwe linawazungulira. Linali gulu lalikulu lomwe linkapanikizana ndi kukankhana ndipo kunali kovuta kuti wina ayende.<br>• Koma nthawi yomweyo, gulu lija linapereka mpata kwa munthu wina wolemekezeka wochokera m'mudzimo amene ankafuna kuonana ndi Yesu. Fotokozani kuti Yairo anali woyang'anira sunagoge, kutanthauza kuti aliyense m'dera limeneli ankamudziwa. ***(Marko 5: 22-23)***<br>• Nthawi yomweyo munthuyu wolemekezeka amene ankalamula ena, anagwa pansi pa mapazi a Yesu kupempha thandizo.<br>• *Fotokozani kuti izi zinali zachilendo kwa anthu oyang'anira sunagoge chifukwa iwo ankadana ndi Yesu ndi ziphunzitso zake, koma iwo ankagwada pamaso pa Mulungu yekha osati pa munthu ayi.*<br>• Yairo ankafunitsitsa thandizo. Mwana wake wamkazi ankadwala kwambiri, ndipo iye ankakhulupirira kuti Yesu akanatha kumuchiritsa. Zochita zake ndi mawu ake anasonyeza kuti ankakhulupirira kuti Yesu anachokera kwa Mulungu. Yesu ankafuna kuthandiza Yairo. Fotokozani kuti Iye amathandiza aliyense amene amabwera kwa Iye. ***(Marko 5: 23)***<br>• Ali pa ulendo wopita ku nyumba yake kunabwera uthenga woti mwana uja wamwalira. Yesu anawuza Yairo kuti akhale ndi chikhulupiriro. Iwo anayendabe kumapita ku nyumba kumene kunali phokoso ndi kulira. Yesu anachotsa anthu m'nyumbamo ndipo anatenga ophunzira ake atatu ndi makolo ake ndi kulowa m'nyumbamo. ***(Marko 5: 38-40)***<br>• Yesu anayankhula kwa mtsikanayo kumuwuza kuti ayimirire. Iye anayimirira ndi kuyamba kuyendayenda. Fotokozani kuti anali atamwalira ndipo kenaka Yesu anamuukitsa. Iye sanali mzukwa kapena china chake. Mtsikanayo anachira ndipo anayamba kuyenda, kuyankhula ndi kudya. ***(Marko 5: 41-43)***<br>• *Fotokozani kuti tikuyenera kumayamika chifukwa cha mphatso ya moyo ndi kutenga kukhala chodabwitsa kukhala ndi moyo ndi kusangalala ndi zinthu zabwino zonse zimene Mulungu watipatsa. Ambuye Yesu akufuna kutipatsa moyo wa mtundu wina – moyo wosatha pamene tamukhulupirira. Pamene tidzadziwa kuti machimo athu akhululukidwa, moyo wathu uli pa ubale wabwino ndi Mulungu ndi tsiku lina tidzakhala Kumwamba - Onani* ***Aroma 6: 23****.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Mtsikana womwalira akhala moyo! |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Marko 5: 42***. |
| **KUMBUKIRANI** | Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:<br>• Kodi ndani anabwera kudzaonana ndi Yesu?<br>• N'chifukwa chiyani Yairo anali munthu wolemekezeka?<br>• Kodi ndi chiyani chachilendo chomwe anachita?<br>• Kodi chinachitika n'chiyani ali pa ulendo?<br>• Kodi ku nyumba anaonako chiyani?<br>• Kodi Yesu anatenga ndani polowa m'nyumba?<br>• Pamene Yesu anayankhula, mtsikanayo anachita chiyani?<br>• Kodi Yesu atha kutipatsa moyo wa mtundu wanji? |

## C3 Nkhani Yoyamba
## Zakeyu – Iyi ndi nkhani ya Yesu kukhala bwenzi lanu.

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Moyo wa Zakeyu unasintha pamene anakumana ndi Yesu.<br>• Ambuye Yesu akufuna kukhala Mpulumutsi ndi Bwenzi lathu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 19: 9***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 19: 1-10*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani momwe amalandirira munthu wofunika kwambiri m'mudzi mwanu. Mwina ana atha kufotokoza zomwe akudziwa. Fotokozani zomwe zimachitika, phokoso ndi zomwe mungaone. |
| **PHUNZITSANI** | • Anthu a ku Yeriko anali atamva kale za Yesu. *Kodi iwo anali atamva chiyani? (Iye anali m'phunzitsi wabwino ndi m'chiritsi... Ganizirani nkhani za mu C2.)*<br>• Pamene Yesu ankadutsa mu mzinda umenewu pa ulendo wopita ku Yerusalemu, anthu ambiri anabwera kwa Yesu kuti aone zomwe angawachitire ndi kunena. Munthu m'modzi amene ankafuna kuona Yesu anali Zakeyu, munthu wachuma komanso mkulu wa amisonkho mu mzindamo. *Funsani ana chifukwa chomwe anthu sankakonda munthu wolandira misonkho. Fotokozani kuti Zakeyu anali munthu wachinyengo chifukwa ankalandira ndalama zambiri kuchokera kwa anthu ndipo ankatengako zina.* ***(Luka 19: 1-2)***<br>• Pamene Zakeyu ankafuna kuona Yesu, anali ndi vuto. Iye anali wamfupi ndipo sakanatha kuona chifukwa cha misinkhu ya anthuwo. *Onetsani kuyimirira ndi zala zanu.* ***(Luka 19:3)***<br>• Zakeyu anapeza njira! Iye anathamanga kupita kutsogolo ndi kukakwera mtengo wamkuyu kuti mwina angaone Yesu. Koma pamene Yesu ankadutsa pansi pa mtengowo anayang'ana m'mwamba, ndipo anaona Zakeyu. *Fotokozani za kudabwa kwa Zakeyu pamene anaona kuti Yesu wayima pamenepo.*<br>• *... Uzani ana zomwe Yesu anayankhula.* Zakeyu anasangalala kwambiri! Iye anatsika mu mtengo ndi kupita ndi Yesu ku nyumba yake. ***(Luka 19: 4-6)***<br>• Anthu anang'ung'udza chifukwa Yesu anapita ku nyumba ya munthu wochimwa. *Fotokozani kuti anthu ankaganiza kuti Yesu sakanapita kwa ochimwa.* Iwo ankati Zakeyu ndi wochimwa. *Kambiranani za mawu oti "wochimwa" ndi kunena kuti tonsefe ndi ochimwa. Tchimo limatilekanitsa ndi Mulungu.* Zakeyu anamvera zimene Yesu ananena ndipo anadziwa kuti ankayenera kusintha. Iye ankafuna kukhala moyo wokondweretsa Mulungu osati wokondweretsa iye. Pofuna kuonetsa kuti anazindikira kulakwa kwake potenga ndalama zomwe sizinali zake anawuza Yesu kuti apereka theka la ndalamazo kwa anthu osauka komanso kupereka ndalama zambiri kuposa zomwe analanda anthu. ***(Luka 19: 7-8)*** Aliyense amene ndi bwenzi ndi wotsatira Yesu adzafuna kumvera Mulungu ndi kusabera ena. ***(Eksodo 20: 15)***<br>• Yesu anawuza Zakeyu akuti "Chipulumutso chafika m'nyumba muno." Kusinthika kwenikweni kunachitika m'moyo wake chifukwa Yesu anamupulumutsa ku tchimo. Kuyambira tsopano, m'mene adzagwirira ntchito yake ndi kuchitira ena zidzakhala zosiyana kwambiri. ***(Luka 19: 9-10)***<br>• *Yesu anabwera kudzatipulumutsa ifenso ku machimo athu. Ngati tilapa zoyipa zomwe tachita pamaso pa Mulungu ndi kumukhulupirira, Iye akulonjeza kutikhululukira machimo athu ndi kuti tikhala nawo m'banja la Mulungu. Tidzafuna kukhala moyo okondweretsa Mulungu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Zakeyu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Luka 19: 9***. Zakeyu anali mwana wa Abrahamu osati chifukwa anali Myuda, koma chifukwa, monga Abrahamu, ankakonda Mulungu ndipo ankafuna kukhala moyo wokondweretsa Iye. Kodi anachita zimenezi motani mu nkhani yathu ya lero? |
| **KUMBUKIRANI** | Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:<br>• Kodi Yesu ankapita kuti?<br>• Kodi Iye ankadutsa mzinda uti?<br>• Kodi Zakeyu ankagwira ntchito yotani?<br>• N'chifukwa chiyani anthu ankadana naye?<br>• Kodi Zakeyu anachita chiyani kuti aone Yesu?<br>• Ankang'ung'udza ndani Yesu atapita ku nyumba ya Zakeyu?<br>• Zakeyu anachita chiyani kufuna kuonetsa kuti moyo wake wasintha atakumana ndi Yesu?<br>• Kodi iye analonjeza kuchita chiyani?<br>• Kodi Yesu anati anabwera chifukwa chiyani?<br>Kapena kalasi ichite sewero la nkhaniyi. M'phunzitsi awerenge Ndime Yowerenga ndipo ana achite magawo a Yesu, Zakeyu, ndi gulu la anthu. |

## C3 Nkhani Yachiwiri

**Nikodemo – Iyi ndi nkhani ya kubadwa m'banja la Mulungu.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Nikodemo ankafuna kuphunzira zambiri za Yesu.
- Ife tikuyenera kubadwanso kuti tikhale ndi moyo wosatha.

**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 3: 16***
**Ndime Yowerenga:** ***Yohane 3: 1-16***

**MAWU OYAMBA**

- Kalasi 1- Mukhale ndi chithunzi cha mwana wakhanda ndi kuyankhula zodabwitsa za moyo watsopano.
- Kalasi 2 - Kodi Mfarisi ndi ndani? *Fotokozani kuti ndi gulu la atsogoleri achipembedzo mu nthawi ya Yesu amene ankaganiza kuti akasunga malamulo a Chiyuda ndi miyambo yake adzalandira moyo wosatha.* Mu nkhani ya lero Mfarisi anali ndi chidwi chofuna kudziwa choonadi pa iye yekha.

**PHUNZITSANI**

- Yesu anali mu Yerusalemu pa phwando la Paskha. Munthu wolemekezeka wa mu mzindamo, Nikodemo, anali ndi chidwi chofuna kudziwa zambiri za Yesu. *Fotokozani kuti ndi chinthu chabwino kufuna kudziwa zambiri za Yesu.* Iye anali atamva kuti Yesu ankachita zodabwitsa ndi kuphunzitsa anthu za Mulungu. Nikodemo anali Mfarisi. (Kalasi 2) Iye anachita chiganizo chopita kukaonana ndi Yesu usiku. *Yankhulani chifukwa chomwe anapitira usiku - mwina sankafuna kuti anthu amuone kapena ankafuna kupita nthawi imene kunalibe anthu ambiri ozungulira Yesu. Werengani zomwe Yesu anayankhula.* ***(Yohane 3: 1-2)***
- Yesu anawuza Nikodemo kuti anthu akuyenera 'kubadwa mwatsopano' kuti akhale ndi moyo wosatha. Nikodemo anadabwa kwambiri. Werengani ***Yohane 3: 4*** *ndipo thandizani ana kuti amvetsetse vuto la Nikodemo.* Yesu anafotokoza kuti sikunali kokwanira kubadwa monga munthu kokha, koma timafunikanso moyo wina watsopano. Timakhala ndi moyo watsopano umenewu pamene tapempha Mulungu kuti atikhululukire machimo athu ndi kukhulupirira Yesu monga Mpulumutsi. *Fotokozani kuti pamene tabadwa, tikhala m'banja lathu. koma tikalandira moyo watsopano wa Mulungu, zimakhalanso ngati kubadwa m'banja latsopano - banja la Mulungu - ndipo timakhala ana a Mulungu.* ***(Yohane 3: 3-4)***
- *Ndi ana a Kalasi 2 muyankhule ndi udindo wa Mzimu Woyera. Yesu anafananitsa Mzimu ndi mphepo. Ife sititha kuona mphepo, koma timaona zomwe imachita. Funsani ana akupatseni zitsanzo. Mzimu Woyera saoneka, koma amakhala akugwira ntchito m'moyo wa munthu amene wamvetsetsa za kubadwa m'banja la Mulungu. Mzimu Woyera ndi Mthandizi ndi Mtsogoleri amene ndi wamoyo ndipo amagwira ntchito m'moyo wa Mkhristu.* ***(Yohane 3: 5-8)***
- Yesu anadabwa kuti Nikodemo sankamvetsa zomwe Iye ankanena. Kunali kovuta kuti Nikodemo amvetsetse zinthu za Kumwamba komabe Yesu anafotokoza kuti Mwana wa Munthu (Iye mwini) anachokera Kumwamba. ***(Yohane 3: 9-13)***
- *Yesu anapitiriza kumukumbutsa Nikodemo za nthawi imene Mulungu anawuza Mose kuti apange njoka yamkuwa ndi kuyipachika pa mtengo m'chipululu kuti Aisrayeli asafe.* ***(B11 Nkhani Yachinayi: Numeri 21: 4-9)*** *Ndi ana a Kalasi 2 mutha kufotokoza zambiri za nkhani imeneyi. Yesu anafotokoza kuti nayenso adzapachikidwa...pa mtanda kuti aliyense amene akhulupirira Iye apulumutsidwe ku tchimo.* ***(Yohane 3:14-15)***
- *Kenaka pakubwera vesi yodziwika kwambiri m'Baibulo ndi Vesi Yoloweza.* ***(Yohane 3: 16)*** *Yankhulani kwa ana za nkhani yabwino ya Mulungu.* Yesu anawuza Nikodemo kuti Mulungu amakonda aliyense pa dziko lapansi kotero anatumiza Mwana wake, Yesu, kudzafa pa mtanda.
- *Munthu amene amakhulupirira Yesu ndi imfa yake kuti kunali kulangidwa m'malo mwa tchimo lathu, amalandira moyo wosatha ndipo tsiku lina adzapita Kumwamba.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**
**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Nikodemo.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Yohane 3: 16***. Onetsani zigawo za vesiyi, pogwiritsa ntchito mitundu yosiyanasiyana. Theka loyamba likutiwuza za Mulungu - Yesu, Mwana, ali pakati - theka lachiwiri likutiwuza zomwe tikuyenera kuchita.

**KUMBUKIRANI**

Konzani mafunso kuchokera pa zimene mwaphunzira.
Kapena ana achite chionetsero cha zinthu zimene Yesu anaphunzitsa Nikodemo. Monga:
- Mwana wakhanda m'manja mwa makolo ake / kubadwa m'banja la Mulungu.
- Mphepo / Mzimu Woyera.
- Njoka pa mtengo / Yesu pa mtanda.
- Chikondi cha Mulungu pa dziko lapansi. Tengani zithunzi za ana amitundu yosiyanasiyana ndi kuyika pa mapu ndi kulembapo ***Yohane 3:16***.

## C3 Nkhani Yachitatu

**Mayi wa ku Samariya – Iyi ndi nkhani ya Yesu kupereka mphatso ya moyo wosatha.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu anakhala ndi nthawi yofotokozera mayi wina za chimene ankachifuna kwambiri kuposa china chilichonse.<br>• Yesu akuyitana aliyense kuti alandire 'madzi amoyo'.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 4: 42***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yohane 4: 4-30, 39-42*** |
| **MAWU OYAMBA** | • Kodi chimatichititsa ludzu ndi chiyani? Funsani ana akupatseni mayankho. Kodi chinthu chabwino chothetsa ludzu ndi chiyani? Yankhulani za kumene mumatunga madzi (mpope, madzi ozizira m'filiji, madzi a m'botolo, pa chitsime, pa mjigo). Yankhulaninso momwe madzi amathetsera ludzu. Mu nkhani yathu lero, Yesu akupempha madzi akumwa! Iye anali munthu ndipo ankamva ludzu ngati ife.<br>• Kapena, kodi mumachita chiyani mukalandira nkhani yabwino? *Funsani ana kuti apereke zitsanzo ndipo ngati akufuna kuwuza ena.* Mayi mu nkhani yathu anali ndi nkhani yabwino yoti akagawane ndi anansi ndi abwenzi ake. |
| **PHUNZITSANI** | • Yesu anali pa ulendo ndi ophunzira ake ndipo anaganiza zodutsa m'dziko la Samariya. *Onetsa ana akulu msinkhu malowo pa mapu.* Iye anafika ku mudzi wa Sukari. Yesu, amene ankamva kutentha ndiponso kutopa, anakhala pansi pa chitsime. *Kwa Kalasi 1*, *afotokozereni zambiri kapena perekani chitsanzo.* Inali nthawi ya masana. Otsatira ake anali atapita kukagula chakudya m'mudzi ndipo Yesu anatsala yekha. ***(Yohane 4: 4-6)***<br>• Atakhala pamenepo, mayi wina anabwera pa chitsimepo kudzatunga madzi. *Fotokozani chifukwa chomwe izi zinali zachilendo – nthawi yobwera kudzatunga madzi inali pamene kukuzizira.* Yesu anafunsa kuti amupatse madzi amwe. *Fotokozani chifukwa chimene mayi (Msamariya) anadabwa kwambiri pamene Yesu (Myuda) anayankhula naye. Ayuda ndi Asamariya sankayankhulana.* ***(Yohane 4: 7-9)***<br>• Yesu anawuza mayiyo kuti akhoza kumupatsa 'madzi amoyo' ndipo iye sadzamvanso ludzu. Mayiyo sanamvetsetse chifukwa Yesu analibe mtsuko wotungira madzi mu chitsimemo. *Fotokozani kuti Yesu sankatanthauza madzi a mu chitsime koma Iye akanamupatsa moyo wosatha kapena 'madzi amoyo'.* ***(Yohane 4: 10-15)***<br>• Yesu anawuza mayiyo kuti ankadziwa zoyipa zonse anakhala akuchita m'mbuyomo. *(Yankhulani molinga ndi msinkhu wa ana.)* Mayiyo anadabwa kwambiri kuti Yesu ankadziwa zambiri za moyo wake! Mayiyo anazindikira kuti Yesu anali mneneri wochokera kwa Mulungu. Atayankhula zinthu zina, Yesu anawuza mayiyo kuti Iye anali amene Mulungu analonjeza kuti adzamutuma kudzapulumutsa anthu ku machimo awo. ***(Yohane 4: 16-26)*** *Fotokozani kuti amene amakhulupirira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu ndi kupempha kuti awakhululukire tchimo lawo, tsiku lina adzapita Kumwamba – iwo adzakhala ndi moyo wosatha.*<br>• Nthawi yomweyi, otsatira a Yesu anabwera. Mayiyu anali wosangalala ndi zimene Yesu anayankhula motero anasiya mtsuko wake ndi kuthamanga kupita kukawuza ena nkhani yabwinoyi. *Werengani zimene ananena.* ***(Yohane 4: 29)***. Anthu a m'mudzimo anapita kukakumana ndi Yesu. ***(Yohane 4: 27-30)***<br>• Atamvetsera zomwe Yesu ankayankhula, Asamariya ambiri anakhulupirira Iye. Iwo anazindikira chimene Iye anali. ***(Yohane 4: 39-42)*** *Werengani Vesi Yoloweza yomwe ikutiwuza ife zomwe iwo anakhulupirira. Kodi inu mumadziwa Yesu monga Mpulumutsi wanu? Kodi munalapa zoyipa zimene mumachita ndi kusankha kutsatira zimene Mulungu amanena m'Baibulo? Ngati munatero, bwanji osawauza ena nkhani yanu yabwino monga anachitira mayi wa pa chitsimeyu?*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjeezera B – Mayi wa ku Samariya. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Yohane 4: 42***, kapena gawo lomaliza kwa ana achichepere. *Fotokozani kuti 'dziko lapansi' akutanthauza anthu okhalamo.* |
| **KUMBUKIRANI** | Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:<br>• Kodi Yesu anayima pati pa ulendo wake?<br>• Kodi Iye anakumana ndi ndani?<br>• Kodi anapempha chiyani?<br>• Kodi Iye anati apereka chiyani kwa mayiyu?<br>• Kodi Yesu amapereka chiyani kwa amene amakonda Iye?<br>• N'chifukwa chiyani mayiyu anachoka ndi kusiya mtsuko wake?<br>• Kodi ndi ndani anabwera kudzaona Yesu?<br>• Kodi iwo anakhulupirira kuti Yesu ndi ndani? |

**C3 Nkhani Yachinayi**

**Mnyamata wachuma – Iyi ndi nkhani ya kutenga Yesu kukhala woyamba.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu anayankha funso la momwe tingapezere moyo wosatha.<br>• Yesu akufuna ife timulole kuti akhale woyamba m'miyoyo yathu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Marko 10: 21***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Marko 10: 17-23*** |
| **MAWU OYAMBA** | • Funsani ana kuti afotokoze chinthu chimene ndi chofunika kwambiri kwa iwo – mwina ndi chidole kapena chiweto. Fotokozani kuti iwo ali ndi mwayi kukhala ndi zinthu zimenezi zomwe amasangalala nazo ndi kuseweretsa. Ndi zinthu zabwino zimene Mulungu wawapatsa. Koma pakatha nthawi mwina adzapezanso zina m'malo mwa zimenezo. N'kofunika kuti Yesu Mwini akhale wofunika kwambiri kwa ife kuposa zinthu zonse zimene tili nazo. Iye amatikonda ndi kutisamalira kwambiri ndipo ndi bwenzi lathu labwino kuposa wina aliyense amene tingakhale naye.<br>• Kumbutsani/yankhulani kwa ana za malamulo a Mulungu. Kodi lamulo loyamba pa khumi aja ndi liti? ***(Eksodo 20: 3)*** – "Usakhale ndi milungu ina koma Ine ndekha." Kodi zikutanthauza chiyani? Mulungu akhale woyamba m'miyoyo yathu. |
| **PHUNZITSANI** | • Tsiku lina, mnyamata wachuma anali ndi funso lofunika kwambiri kwa Yesu. Choncho anathamangira Yesu pamene Iye ankayenda mu msewu ndi kugwada pansi pamaso pake. Mukuganiza n'chifukwa chiyani anagwada pamaso pa Yesu? *(Iye ankadziwa kuti Yesu anali munthu wolemekezeka.) Kambiranani zomwe anafunsa.* Mnyamata ameneyu anali ndi ndalama zambiri ndipo akanatha kugula zovala zonse zabwino, kukhala m'nyumba yayikulu ndi kukhala ndi zinthu zonse akanazifuna. Koma kuonjezera pa zimenezi, iye ankafuna kudziwa momwe angapezere chitsimikizo kuti tsiku lina adzapita Kumwamba. ***(Marko 10: 17)***<br>• Yesu sanayankhe funso lake mwachindunji. Yesu anamukumbutsa mnyamatayu za malamulo ena a Mulungu. *Kodi mukumbukira kuti amatchedwa chiyani? (Malamulo Khumi) Funsani ana ngati akukumbukira limodzi la malamulowa lomwe limanena momwe tikuyenera kuchitira anthu ena. Tchulani amene Yesu ananena.*<br>• Mnyamatayo anawuza Yesu kuti iye wakhala akusunga wonse kuyambira ali mwana. ***(Marko 10: 18-20)*** *Fotokozani kuti mnyamatayu sankaganiza kuti anachita cholakwika. Iye sankadziwa kuti anali wochimwa ndi kuti anaphwanya malamulo a Mulungu. Tonse tinaphwanya malamulo a Mulungu. Palibe wina aliyense, kupatula Yesu yekha, amene ali wangwiro.*<br>• Yesu anayang'ana mnyamatayu ndipo anamukonda. Kenaka anamuyesa mnyamatayu kuti aone ngati watsimikiza mtima zakukhala ndi moyo wosatha. Izi zikutanthauza kuti tsiku lina akanadzapita Kumwamba ndi kukakhala ndi Mulungu kwamuyaya. Fotokozani zomwe Yesu anamuwuza kuti achite. *Fotokozani kuti 'chuma Kumwamba' zikutanthauza kuti tsiku lina mnyamatayo adzakhala ndi moyo wosatha.* Yesu ankafuna kuona ngati ndalama za mnyamatayo ndi zonse zimene anali nazo ndiye zofunika kuposa kutsatira Iye. ***(Marko 10: 21)***<br>• Baibulo limatiwuza kuti nkhope ya mnyamatayo inali yachisoni. Mayeso anali okhwima kwambiri. Iye sanafune kusiyana ndi zonse zimene anali nazo chifukwa anali ndi chuma chambiri. Iye anachoka ndipo sanakhale wotsatira wa Yesu. Iye sanali wokonzeka kutenga Yesu kukhala woyamba kuposa chilichonse pa moyo wake. Mnyamatayo atapita, Yesu anawuza otsatira ake kuti ndi kovuta kuti munthu wachuma akalowe mu ufumu wa Mulungu chifukwa amakonda zimene ali nazo pa dziko lapansi kuposa Yesu.<br>• *Kodi inu munayika Yesu kukhala woyamba m'moyo wanu?* ***(Marko 10: 22-23)***<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mnyamata wachuma. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Marko 10: 21***, kapena gawo lina kwa anawo. |
| **KUMBUKIRANI** | Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:<br>• Kodi mnyamatayu anaonetsa motani kuti ankadziwa kuti Yesu anali munthu wolemekezeka?<br>• Kodi iye anafunsa chiyani?<br>• Tchulani lamulo lililonse limene Yesu anatchula.<br>• Kodi mnyamata ananena chiyani za malamulo amenewa?<br>• Kodi Yesu anamuwuza mnyamatayo kuti achite chiyani pofuna kuonetsa kuti Yesu anali wofunika kuposa ndalama zake?<br>• Kodi anakhoza kapena analephera mayeso? Chifukwa chiyani? |

## C4 Nkhani Yoyamba
**Nkhani ya Paskha: Yudase – Iyi ndi nkhani ya kuperekedwa kwa Yesu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yudase anapereka Yesu ndi ndalama zasiliva makumi atatu.<br>• Yesu analola adani ake amugwire chifukwa ankadziwa kuti zomwe zinali patsogolo pake chinali chikonzero cha Mulungu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 26: 24***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Mateyu 26: 14-16 ndi 36-50*** |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana ngati akukumbukira zodabwitsa zimene Yesu anachita kapena kutchula anthu amene anawathandiza mu C2. Kodi akukumbukira anthu amene anakumana nawo ndi kuyankhulana nawo mu C3? Kodi ndi ziti zazikulu zimene Yesu anayankhula nawo? (moyo wosatha/ kukhululukidwa) Awuzeni kuti chifukwa chimene Yesu anabwera pa dziko lapansi chinali choposa machiritso kapena chiphunzitso. Anabwera kudzakwaniritsa chikonzero cha Atate ake choti afe pa mtanda kuti machimo athu akhululukidwe ndipo tikhale ndi moyo wosatha. |
| **PHUNZITSANI** | • Akulu a ansembe ndi atsogoleri a anthu anagwirizana zopeza njira yophera Yesu. Yudase, m'modzi mwa ophunzira a Yesu, anapita ndi kuwalonjeza kuti adzawatsogolera kumene kunali Yesu. Iwo anamupatsa ndalama zasiliva makumi atatu kuti 'apereke' Yesu. *Fotokozani tanthauzo la mawu akuti 'kupereka'. Kambiranani kuti Yudase anapereka Yesu chifukwa ankafuna ndalama kuposa kutsatira Yesu. Iye sankakonda Yesu ndipo sanali wotsatira weniweni.* ***(Mateyu 26: 14-16)***<br>• Madzulo ena, Yesu anapita ndi ophunzira ake, kupatula Yudase, ku Munda wa Getsemane. M'mundamo, Yesu anafunsa Petro, Yakobo ndi Yohane kuti akhale maso pamene Iye ankapita kukapemphera kwa Atate ake, Mulungu. Yesu ankadziwa chomwe chichitike. Baibulo limatiwuza kuti Iye anayamba kumva 'chisoni ndi kuvutika' mu mtima. *Kodi ankamva zimenezi chifukwa chiyani?* Ngakhale ankadziwa zomwe zidzachitike, Iye anapemphera kuti, "Osati kufuna kwanga, koma kufuna kwanu kuchitike." *Fotokozani kuti Yesu anali wokonzeka kuchita chifuniro cha Mulungu ndi kulola kuti apachikidwe chifukwa cha chikondi chake pa ife ndiponso wokonzeka kulangidwa chifukwa cha machimo athu.* ***(Mateyu 26: 36-39)***<br>• Pamene Yesu ankapemphera, ophunzira anagona tulo. Izi zinachitika katatu ndipo nthawi iliyonse Yesu anabwera kudzawadzutsa. Kenaka, Yesu anadziwa kuti nthawi yakwana kuti achite chifuniro cha Mulungu. ***(Mateyu 26: 40-46)***<br>• *Fotokoza za phokoso la mapazi a anthu lomwe linkamveka mu mdima.* Anali Yudase pamodzi ndi gulu la anthu amene ananyamula malupanga ndi zibonga. *Kodi mukuganiza ankafuna kuchita chiyani?* Fotokozani kuti kunali kovuta kuzindikira nkhope za anthu mu mdima koma Yudase ankamudziwa Yesu ndipo anapita pamene anali ndi kumupsopsona. Izi zinachititsa kuti adziwe amene ankayenera kumugwira. Yesu analola kuti anthuwo amugwire. Kenaka Iye analola kuti anthuwo amugwire. ***(Mateyu 26: 47-50)***<br>• Yudase anachita choyipa chachikulu popereka Yesu. *Popanda kupereka zitsanzo, yankhulani ndi ana za kuyipa za kukhumudwitsidwa ndi munthu wina amene ife tinkamudalira.* Yudase ankafuna ndalama kuposa mmene ankafunira kutsatira Yesu.<br>• Yesu amatikonda kwambiri ndipo anali wokonzeka kumva chisoni chachikulu pamene ankapemphera m'munda ndi kuperekedwa ndi mnzake wachinyengo. Izi zinali mu zinthu zimene ankayenera kukumana nazo pamene ankakwaniritsa chikonzero cha Mulungu kwa ife. Posachedwa Yesu alandira chilango chonse cha machimo athu.<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera – Yudase. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Mateyu 26: 24***. Ana a Kalasi 1 aphunzire gawo loyamba la vesili. |
| **KUMBUKIRANI** | Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:<br>• Kodi ndi ndani anakonza chiwembu chofuna kupha Yesu?<br>• Kodi dzina lake ndani wophunzira amene anapereka Yesu?<br>• Kodi mawu akuti 'kupereka' amatanthauza chiyani?<br>• Kodi anamupatsa Yudase ndalama zasiliva zingati?<br>• Kodi dzina la munda umene Yesu anapita kukapemphera ndi chiyani?<br>• Kodi chinkachitika ndi chiyani pamene Yesu ankapemphera?<br>• Kodi Yudase anaonetsa motani anthu aja kuti uyu ndi Yesu?<br>• N'chifukwa chiyani Yesu analola kuti amugwire? |

## C4 Nkhani Yachiwiri

**Nkhani ya Paskha: Pilato – Iyi ndi nkhani ya kufa kwa Yesu pa mtanda.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu anali wosalakwa.<br>• Yesu anafa chifukwa cha machimo athu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 27: 22***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Mateyu 27: 1-2 ndi 11-31*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsanani nkhani ya m'mbuyo ndi ana. Yesu anamangidwa ndi gulu limene analitumiza atsogoleri a Chiyuda. Funsani ana ngati anakhala pa mavuto chifukwa cha zinthu zimene iwo sanachite. Mwina analangidwa ngakhale kuti sanachite cholakwika. Kodi izi zinali zabwino? Kodi zimene zinachitikazo iwo anamva bwanji m'mitima mwawo? Mu nkhani yathu ya lero, ganizirani kuti muone momwe zinalili kwa Yesu, Mwana wa Mulungu wopanda tchimo, kunena kuti anali wolakwa. |
| **PHUNZITSANI** | • Yesu anamangidwa ndipo anapita naye kwa Pilato, Bwanamkubwa wa Chiroma. *Fotokozani kuti atsogoleri a Chiyuda anapita ndi Yesu kwa Pilato chifukwa ndiye ankalamulira dzikolo nthawi imeneyi.* ***(Mateyu 27: 1-2)***<br>• Pilato anafunsa mafunso Yesu. Iye anali ndi chitsimikizo kuti Yesu anali wosalakwa. *Kumbutsani ana kuti Yesu sanachitepo tchimo lililonse. Iye anali wopanda tchimo.* Pilato ankadziwa kuti atsogoleri a Chiyuda ankafuna kuti Yesu apachikidwe chifukwa cha nsanje. Iwo anayankhula zambiri zabodza za Yesu. Pilato sanafune kuti apereke Yesu kuti akapachikidwe choncho anapereka mwayi woti amasule wam'ndende m'modzi. Iye anati Ayuda asankhe munthu amene akufuna kuti awamasulire. Pilato ankayembekezera kuti iwo asankha Yesu koma sanatero. Iwo anasankha Baraba, amene anali munthu woyipa, ndipo anafuula kuti Yesu apachikidwe. *Funsani kuti, 'Kodi Yesu anali woyenera kupachikidwa? Kodi mukuganiza kuti izi zinali zabwino?' Kambiranani chifukwa chomwe Mulungu analolera kuti anthu amuchitire zimenezi Yesu.* ***(Mateyu 27: 11-23)***<br>• Pilato anadziwa kuti anthuwo sasintha maganizo awo. Iye anamasula Baraba ndi kulamula kuti Ambuye Yesu akwapulidwe ndi kutengedwa kukapachikidwa. Asanamupachike, asilikali anamuzunza kwambiri. Iwo anamuveka mkanjo wofiira ndi kumuveka chipewa cha minga pa mutu pake. Iwo anamunyoza, kumulavulira ndi kumumenya. Kenaka anamupachika pomukhoma misomali pa mtanda. ***(Mateyu 27: 24-31)***<br>• **Kalasi 2-** *Mutha kufotokoza zifukwa zina zimene Yesu anafera. Zikuoneka ngati sizinali zoyenera kuti munthu woyipa ngati Baraba amasulidwe ndipo Yesu amene sanachite choyipa akaphedwe. Fotokozani kuti Mulungu ndiye ankalamulira zochitika ngakhale zinkaoneka kuti anthuwo ndiwo anali ndi mphamvu pa Yesu. Yesu anali atafotokozera kale ophunzira ake kuti Iye adzafa motere ngakhale sankamvetsetsa.* ***(Mateyu 16: 21; 17: 22-23; 20: 17-19)*** *Aneneri a m'Chipangano Chakale nawonso analemba za zinthu zimenezi zisanachitike. Tsopano zinakachitika monga m'mene Mulungu anakonzera.*<br>• **Kalasi 1 ndi 2-** *Yesu sanali woyenera kufa. Iye anafa mwaufulu wake chifukwa cha kutikonda ife ndipo anafuna kulangidwa chifukwa cha machimo athu. Yesu anafera machimo a dziko lonse lapansi. Inali nthawi yopambana kwambiri m'mbiri ya dziko lapansi, koma aliyense wa ife akuyenera kuchitapo kanthu pa yekha. Tikatembenuka mtima ndi kukhulupirira Yesu, Iye adzatikhululukira ndi kuchotsa machimo. Ndipo pamenepo tidzakhala ndi chitsimikizo chakuti tsiku lina tidzakakhala naye Kumwamba.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Pilato. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Mateyu 27: 22.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Lembani Zoona/Zabodza pa ziganizo izi:<br>• Pilato anafunsa mafunso Yesu.<br>• Pilato ankaganiza kuti Yesu anali wolakwa.<br>• Atsogoleri a Chiyuda sankafuna kuti Yesu apachikidwe.<br>• Yesu sanachitepo tchimo lililonse.<br>• Baraba anali munthu wosalakwa.<br>• Asilikali anamuchitira chifundo Yesu.<br>• Yesu analangidwa chifukwa cha machimo athu.<br>• Ife titha kudzakhala Kumwamba ndi Yesu ngati takhululukidwa machimo athu. |

## C4 Nkhani Yachitatu

**Nkhani ya Paskha: Yosefe – Iyi ndi nkhani ya Yesu kuuka kwa akufa.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Yesu anayikidwa m'manda ndipo anaukanso.<br>• Mphamvu yayikulu ya Mulungu ndiye inaukitsa Yesu kwa akufa.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 28: 6***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Mateyu 27: 57-66*** |
| **MAWU OYAMBA** | Onaninso maphunziro awiri a m'mbuyo. Pamene ana akufotokoza zomwe zinamuchitikira Yesu, lembani mawuwo pa pepala ndi zithunzi kapena pa khoma monga m'mene akufotokozera.<br>**kuperekedwa kumangidwa kufunsidwa kuweruzidwa kunyozedwa kupachikidwa**<br>Kodi angathe kulemba mwandondomeko yoyenera? Khazikikani pa chifukwa chomwe izi zinachitika. |
| **PHUNZITSANI** | • Yesu anafa pa mtanda. Madzulo a tsiku limenelo, munthu wachuma wotchedwa Yosefe anapita kukayankhula ndi Pilato. Yosefe ankakhulupirira Yesu ndipo anapempha Pilato kuti amulole kutenga thupi la Yesu kuti akaliyike ku manda moyenera. ***(Mateyu 27: 57-58)***<br>• Yosefe anatenga thupilo ndi kulikulunga mu nsalu yabwino ndi yosalala ndipo analiyika m'manda atsopano. Manda ake anali ngati phanga laling'ono pa mwala. Iye anagubuduza mwala waukulu ndi kutseka mandawo ndipo anachokapo. Amayi ena amene ankatsatira Yesu anatsalira pa mandapo. *Funsani ana akufotokoze zomwe akuganiza kuti Yosefe ndi amayi ankamva m'mitima mwawo.* ***(Mateyu 27: 59-61)***<br>• *Fotokozerani ana kuti zaka zambiri za m'mbuyomo izi zisanachitike mneneri Yesaya analosera za kuti Yesu adzayikidwa m'manda a munthu wachuma.* ***(Yesaya 53: 9)*** *Ulosi umenewu apa unakwaniritsidwa.*<br>• Ayuda anali ndi nkhawa ya kuti mwina ophunzira ake abwera usiku kudzaba thupi lake kenaka ndi kumanena kuti Yesu wauka kwa akufa. Iwo anapempha Pilato ngati akanawalola kuti atumize alonda kuti akamate mandawo ndi kuwateteza. ***(Mateyu 27: 62-66)***<br>• Asilikali analondera manda koma sanathe kuletsa mngelo wa Ambuye kubwera kuchokera Kumwamba. Iye anagubuduza mwala ndi kuukhalira. M'manda munalibe Yesu! Mngelo anati, "Iye muno mulibe, wauka monga m'mene ananenera." ***(Mateyu 28: 1-6)***<br>• Nkhani yabwino ndi ya kuti Mulungu mwa mphamvu yake yayikulu anaukitsa Ambuye Yesu kwa akufa. Thupi lake silinabedwe. Silinaole. Mulungu anamutulutsa m'manda wamoyo! Izi zikutsimikizira kuti Mulungu ankakondweretsedwa ndi zimene Ambuye Yesu anachita pamene anafera machimo athu. *Kumbutsani ana kuti izi zikusonyezanso kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu. Iye akufuna aliyense amukhulupirire kukhala Mpulumutsi wawo.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Yosefe. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Mateyu 28: 6***. |
| **KUMBUKIRANI** | Zochita za Paskha<br>Gawani kalasi m'magulu atatu. Gulu lililonse likhale ndi ndondomeko yosavuta ya sewero.<br>1) Mitanda itatu. 2) Manda pa khomo ataseka ndi mwala.<br>3) Manda pa khomo atachotsapo mwala.<br>Gwiritsani ntchito mapepala akutha kapena china chilichonse chomwe gulu lingapange. Mulembepo vesi mukapachika zinthuzo. ***(1 Akorinto 15: 3-4)***<br>Kagulu kochepa kakhoza kungochita za gawo lachitatu la sewero. |

## C4 Nkhani Yachinayi

**Nkhani ya Paskha: Anthu awiri a paulendo — Iyi ndi nkhani ya Yesu kuti ali ndi moyo!**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Zonse zinamuchitikira Yesu chinali chikonzero cha Mulungu.<br>• Kuuka kwake kumabweretsa chimwemwe chachikulu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 24: 26***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 24: 13-35*** |
| **MAWU OYAMBA** | Zochita Zobwereza: Ganizani, Akhale awiri, Gawanani.<br>Pangani makadi okhala ndi dzina limodzi pa iliyonse – Yudase, Pilato, Yosefe, amayi. Muyenera kukhala ndi okwanira kuti mugawe limodzi pakati pa ana awiri.<br>Ali awiri, ana afotokozerane kuti **ndani**, **chiyani** ndi **kuti** mogwirizana ndi dzina mu nkhaniyi. M'phunzitsi asankhe ana awiriawiri angapo kuti afotokozere gulu lonse pamapeto. |
| **PHUNZITSANI** | • Awiri mwa otsatira Yesu (m'modzi wotchedwa Kleopa) ankayenda kuchokera ku Yerusalemu kupita ku mudzi wa Emau, ulendo wa makilomita khumi ndi imodzi. Iwo ankayankhula zonse zimene zinachitika mu Yerusalemu ndipo anali achisoni ndi okhumudwa. *Kambiranani chifukwa chake. Fotokozani kuti Yesu anali atauka kwa akufa, koma otsatira awa anali asanamuone.* ***(Luka 24: 13-14)***<br>• Nthawi yomweyo, munthu wachilendo anafika pakati pawo ndipo ankafuna kudziwa zimene ankakambirana. *Fotokozani kuti inu mukhala Kleopa kuyankhula kwa munthu wachilendo. Onetsani chisoni ndi kukhumudwa:*<br>• Kodi inu simunamve zimene zachitika mu Yerusalemu? Mwini ndi inu nokha amene simunamve! Yesu wa ku Nazarete anali mneneri wochokera kwa Mulungu ndipo ife tinkayembekezera kuti iye ndiye Mpulumutsi wochokera kwa Mulungu. Iye anayankhula ndi kuchita zinthu zambiri zodabwitsa. Koma masiku atatu apitawo, atsogoleri athu anamuphera pa mtanda. Lero amayi ena atiwuza nkhani yodabwitsa. M'mamawa lero, iwo anapita ku manda kumene Iye anayikidwa koma sanapezeko thupi lake. Iwo anatiwuza kuti kunali angelo amene ananena kuti Yesu ali moyo! Kenaka anzathu ena anapita ku mandako ndipo anakapeza m'manda mopanda kanthu, monga m'mene amayiwo anafotokozera, ndiponso munalibe chizindikiro cha Yesu! ***(Luka 24: 15-24)***<br>• *Imani ... ndipo fotokozani kuti muyankhula zomwe munthu wachilendo anayankha...* Inu anthu opusa ndi ochedwa kuzindikira choonadi! Inu mukuyenera kukhulupirira zonse zimene aneneri ananena ndi zimene zinalembedwa m'Malemba. Amene Mulungu anamutuma ankayenera kusautsidwa.<br>• *Munthu wachilendowo anafotokoza za kukwaniritsidwa kwa zonse zimene Mulungu anayankhula m'Chipangano Chakale kudzera mwa aneneri. Otsatira awiri a Yesu anadabwa kuti wachilendoyu akudziwa zonsezi!* ***(Luka 24: 25-27)***<br>• Mosakhalitsa, atatuwa anafika ku Emau. Kunali kutada, choncho anakakamiza wachilendo uja kuti akhale nawo usiku umenewo. Pamene ankadya, wachilendo uja anatenga chakudya, anachinyema ndi kuyamika Mulungu. *Kodi apa mukuzindikira kuti wachilendoyu anali ndani?* Baibulo limanena kuti maso awo anatsekuka ndipo anazindikira kuti anali Yesu! Mwadzidzidzi Iye anasowa pakati pawo koma tsopano anali ndi chitsimikizo chonse kuti Yesu wauka kwa akufa! Iwo anazindikira kuti ankamva bwino mu mtima mwawo pamene Iye ankawafotokozera za Iye mwini mu msewu muja.<br>• *Siyanitsani chimwemwe ndi kudabwa kumene anali nako pano kusiyana ndi poyamba paja.* ***(Luka 24: 28-32)***<br>• Nthawi yomweyo ananyamuka kubwerera ku Yerusalemu ndi kukapeza ophunzira aja. Iwo anawawuza zomwe ankafotokoza mu msewu ndipo kuti kenaka iwo anadzazindikira kuti anali Yesu. ***(Luka 24: 33-35)***<br>• *Mu nkhani iyi, otsatira awiri akuphunzira kuchokera kwa Yesu za chikonzero cha Mulungu ndi kukwaniritsidwa kwake. Ifenso tikuyenera kusangalala kuti tikumvetsetsa kuchokera m'Baibulo za Yesu kuti anatikonzera njira yoti tibwerere kwa Mulungu. Iye ankayenera kusautsidwa ndi kufa, kulangidwa chifukwa cha machimo athu. Chinalinso chikonzero cha Mulungu kuti aukenso ndi kubwerera Kumwamba. Baibulo limatiphunzitsa kuti ife tikuyenera kumayamika pa zonse zimene anatichitira kuti machimo athu akhululukidwe, ndipo titha kukhala ndi chiyembekezo kuti tidzakhala naye Kumwamba.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Anthu awiri a paulendo. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Luka 24: 26***. |
| **KUMBUKIRANI** | Zochita gulu: Konzekera nkhani yokhala pa mapepala kuti alumikize bwino ziganizo. Gulu loyamba kutsiriza molondola ndiye limene lipambane. Ziganizo zake ndi izi. Awiri mwa otsatira Yesu akuyenda kupita ku Emau - Iwo anali ndi chisoni - Munthu wachilendo akuyenda nawo - Wachilendo akuyankhula za zomwe zachitika - Ku Emau wachilendo akukhala nawo pa chakudya - Iwo akuzindikire kuti anali Yesu pamene ananyema buledi - Iwo anadzazidwa ndi chimwemwe chifukwa Yesu anali moyo.<br>**Kalasi 1:** Ana ajambule zithunzi za anthu akuyenda mu msewu kapena akudya pamodzi pamene anafika ku Emau. |

## C5 Nkhani Yoyamba
**Rute – Iyi ndi nkhani ya kudalira Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Rute anadalira Mulungu pamene anachita chisankho chopita ku Betelehemu.<br>• Mulungu akufuna kuti ife timukhulupirire.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Rute 1: 16-17***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Rute 1*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za zisankho zimene timachita tsiku ndi tsiku ndi kupereka zitsanzo. Molingana ndi gulu lanu, mutha kupereka mpata kwa aliyense kuti achite chisankho: monga, pakati pa zochita/masewera kapena pakati pa nthawi yopuma.<br>Nkhani ya lero muli anthu osiyana amene anachita zisankho. Limbikitsani ana kuti amvetsere mwatcheru ndi kuona zisankho zonse zimene zinachitika mu nkhaniyi. M'modzi mu nkhaniyi anachita chisankho chomwe chinasintha moyo wake wonse! |
| **PHUNZITSANI** | • Kunali njala *(fotokozani tanthauzo la njala)* ku Betelehemu. Munthu wina wotchedwa Elimeleki anaganiza kuti kunali bwino kutenga mkazi wake ndi ana ake aamuna awiri ndi kupita nawo ku dziko lotchedwa Moabu. ***(Rute 1: 1-2)***<br>• Mwachisoni, Elimeleki anamwalira. Ana ake awiri aamuna anakula ndipo aliyense anaganiza zokwatira mtsikana wa ku Moabu. Pa nthawi yochepa, anyamata aja anamwaliranso! *(Kalasi 2 – tchulani mayina awo)* Tsopano anatsala Naomi yekha ndi akazi amasiye awiri achichepere, Oripa ndi Rute. *Kambiranani mosamala mmene atatu amenewa ankamvera m'mitima mwawo. (Rute 1: 3 -5)*<br>• Pasanapite nthawi yayitali, Naomi anaganiza zobwerera kwawo ku Betelehemu. Iye ananyamuka pamodzi ndi Oripa ndi Rute amene ankafuna kupita naye. Naomi anawawuza kuti kunali bwino akanatsala ku Moabu, m'dziko lawo. Oripa anachita chiganizo chobwerera kwawo. Koma Rute sanasinthe maganizo ake. *Kambiranani kuti ichi chinali chisankho chonyeza "kulimba mtima" kwa Rute; Iye akakhala mlendo ku Betelehemu ndipo akakhala wopanda zinthu zambiri zomuthandiza. Werengani mawi ake pa* ***Rute 1: 16-17*** *ndi kufotokoza momwe chisankho ichi chikuonetsa kuti ndi wokonzeka kukhala moyo watsopano pakati pa anthu achilendo koma kuposa zonse kukhala moyo wodalira Mulungu wamoyo ndi woona amene anamudziwa kuchokera kwa Naomi.* ***(Rute 1: 5-16)***<br>• *Fotokozani kuti Mulungu akufuna ife kuti tiphunzire kuchokera pa chitsanzo cha Rute. Iye ndiye anatipanga ndipo amadziwa chimene ndi chabwino kwa ife. Iye akufuna ife kuti timukhulupirire ndi kumulola kuti akwaniritse cholinga chake pa miyoyo yathu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Rute. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Rute 1: 16-17***. Fupikitsani vesi ngati n'koyenera kutero. |
| **KUMBUKIRANI** | Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:<br>1. N'chifukwa chiyani Elimeleki anasankha zochoka ku Betelehemu?<br>2. Kodi iye anali ndi ana aamuna angati?<br>3. Kodi ndi amayi angati amene ananyamuka kupita ku Betelehemu?<br>4. Kodi ndani anabwerera ku Moabu?<br>5. Kodi ndi ndani anapitiriza ulendo ndi Naomi?<br>6. Kodi gawo lofunika kwambiri la chisankho cha Rute linali lotani?<br>7. Kodi vuto la chisankho cha Rute likanakhala lotani?<br>8. Funso kwa ana: Kodi mu nkhani imeneyi atchulamo zisankho zingati? (7) Ana akumbukire zisankho zimenezi. |

<u>**C5 Nkhani Yachiwiri**</u>

**Rute ndi Boazi – Iyi ndi nkhani ya chikonzero cha Mulungu pa Rute.**

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Mulungu anali wabwino kwa Rute ndipo anakwaniritsa chikonzero chake pa iye.
- Mulungu ali ndi chikonzero pa miyoyo yathu.

**Vesi Yoloweza:** ***Rute 4: 13*** *(kapena* ***Aroma 8:28)***
**Ndime Yowerenga:** ***Rute 2-4***

**MAWU OYAMBA**

Onaninso mfundo za nkhani ya sabata yatha. Yankhulani za nthawi yokolola. Kodi mungatchule mbewu zina? Onetsani zithunzi/zitsanzo. Yankhulani za momwe amakololera mbewuzo. Mu nthawi ya Baibulo, kunalibe zipangizo zamakono. Anthu okolola ankagwiritsa ntchito mipeni yayikulu yotchedwa zisenga podula tirigu. Anthu osauka ankakhunkha m'munda umene awalola pambuyo pa okolola ndipo ankatola tirigu aliyense amene watsalira.

**PHUNZITSANI**

- Pamene Rute ndi Naomi anafika ku Betelehemu inali nthawi yokolola barele. Rute ankafuna kugwira ntchito yokhunkha kuti apeze chakudya cha Naomi ndi iye mwini. *Kambiranani kuti ntchito iyi inali yotani (yovuta, osadziwana ndi munthu wina aliyense)*. Mwina Rute anadabwa kwambiri pamene anaona mwini munda, munthu wotchedwa Boazi, kuti anamukomera mtima. Iye anawuza Rute kuti akhale ndi atsikana antchito ake m'mundamo ndipo adzimwa madzi awo akamva ludzu. ***(Rute 2: 8-9)***
- Rute anadabwa kwambiri chifukwa chomwe ankamukomera mtima munthu wachilendo, koma Boazi anafotokoza kuti anali atamva kale za iye! *Funsani ana aganizire zomwe iye anali atamva za Rute.* Boazi ankadziwa kuti Rute ankadalira Mulungu. Mulungu ankagwiritsa ntchito Boazi posamalira Rute. ***(Rute 2: 10-17)*** Pambuyo pake, Boazi anamupatsa Rute chakudya cha masana ndipo anawuza antchito ake kuti azisiyako zina kuti Rute azitola.
- *Funsani ana zomwe Rute anakawuza Naomi pamene anapita kwawo madzulo amenewo. Fotokozani kuti Naomi ankadziwa kuti zonse zimene akuchita Boazi ndi kukoma mtima kwa Mulungu.* ***(Rute 2: 18-23)***
- *Lembani mwachidule kutha kwa nkhani* ***(Rute 3 ndi 4)*** *pofotokoza kuti Mulungu anali ndi chikonzero china ndi moyo wa Rute.* Pasanathe nthawi Rute anakwatiwa ndi Boazi. Pambuyo pake, Rute anabereka mwana wamwamuna amene anamutcha Obedi. *Fotokozani kuti iye anali kholo la Mfumu yayikulu Davide. Yankhulani kuti izi zinachititsa Rute ndi Naomi kukhala osangalala kwambiri – siyanitsani ndi kale. Thandizani ana kuti aone kuti zomwe anachita Rute kusankha Mulungu* ***Rute 1: 16*** *chinali chisankho chabwino. Fotokozani kuti pamene tikudalira Mulungu, Mulungu adzakwaniritsa zolinga zake zabwino ndi zoyenera pa ife.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**
**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Rute ndi Boazi.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Rute 4: 13 kapena Aroma 8: 28***. Mulungu anagwiritsa ntchito zisankho zimene Rute anachita ngakhale anakumana ndi zovuta (kukhala mlendo m'dziko lina) kuti chikonzero chake chikwaniritsidwa pa iye.

**KUMBUKIRANI**

**Kalasi 1** – Nazi ziganizo Zoona/Zabodza zotikumbutsa nkhaniyi:

1. Naomi ndi Rute anafika mu nthawi ya mphukira.
2. Iwo anayamba kugwira ntchito ya m'minda.
3. Rute ankagwira ntchito m'munda wa Boazi.
4. Boazi anasamalira Rute poonetsetsa kuti ali ndi chakudya ndi madzi akumwa.
5. Naomi sankamvetsa chifukwa chimene Boazi ankakomera mtima Rute.
6. Pambuyo pake Boazi anakwatira Rute ndipo anabereka mwana wamwamuna.

**Kalasi 2** – Mutha kukambirana za ziganizo izi:

1. Rute anakhala moyo wofewa atafika ku Betelehemu ndi Naomi.
2. Zinthu zabwino zinamuchitikira mwa mwayi.
3. Mulungu amagwiritsa ntchito anthu ena pofuna kukwaniritsa chifuniro chake pa miyoyo yathu (ganizirani za Naomi ndi Boazi pa moyo wa Rute).

## C5 Nkhani Yachitatu

**Hana apemphera kwa Mulungu – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kuyankha pemphero.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Mulungu anamva pemphero la Hana.<br>• Mulungu akufuna ife tizipemphera.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 7:7***<br>**Ndime Yowerenga:** ***1 Samueli 1: 1-20*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za pemphero. Ana ali ndi muyeso osiyanasiya wa m'mene amamvera zoti pemphero ndi chiyani. Athandizeni kuti achotse maganizo a kuti ndi kukhala ndi zofuna zako. Koma kuti ndi Mulungu Atate athu a Kumwamba amene amafuna kutipatsa zinthu zomwe ndi zabwino kwambiri kwa ife. Fotokozani kupambana kotha kumayankhula ndi Mulungu ndi kudziwa kuti akumvetsera. Ndi ana a Kalasi 2, mutha kuona zinthu zimene zatchulidwa pa pepala la pemphero. |
| **PHUNZITSANI** | • Fotokozani nyengo imene Hana ankadutsamo. *(gawo loyamba la phunziro la Kalasi 2)* ***(1 Samueli 1: 1-2)***<br>• Chaka chilichonse Elikana ankatenga banja lake pa ulendo wapadera opita ku Silo, kumene ankapembedza Mulungu. Koma nthawi iyi, Hana anali wokhumudwa kwambiri chifukwa Penina ankayankhula mawu achipongwe kwa iye chifukwa analibe mwana. Iye ankalira ndipo anakana kudya. Hana anachita chinthu chabwino kwambiri. Iye anaganiza zopemphera kwa Mulungu. *Fotokozani kuti tikuyenera kumafotokozera Mulungu nkhawa zathu ndi mavuto athu.* ***(1 Samueli 1: 3-7)***<br>• Pamene Hana ankapemphera analonjeza kwa Mulungu: Ngati Mulungu amupatsa mwana wamwamuna, iye adzamupereka kwa Mulungu kuti azidzatumikira. Wina wake ankaona! Eli, wansembe, ankaona kuti Hana akulira koma atayang'anitsitsa anaona milomo yake ikugwedera koma sankamva zimene ankayankhula. Eli ankaganiza kuti waledzera, choncho anamudzudzula! Hana anafotokozera Eli kuti anali ndi chisoni chachikulu ndipo ankapemphera kwa Ambuye. *Fotokozani momwe tingapempherere kuchokera mu mtima mwathu monga Hana. Sikofunika kuti tizichita kufuula kwa Mulungu. Mulungu amadziwa zomwe tikutanthauza m'mapemphero athu.* ***(1 Samueli 1: 9-16)***<br>• Kenaka Eli anati kwa Hana, "Pitani mu mtendere, ndipo Mulungu wa Israyeli akupatseni zimene mwamupemphazo." *Funsani ana kuti aganize momwe Hana ankamvera mu mtima mwake tsopano ndiponso yankhulani za kusintha kumene kumabwera tikamuwuza Mulungu mavuto athu.* ***(1 Samueli 1: 17-18)***<br>• Patapita nthawi, Mulungu anayankha pemphero la Hana. Iye anabereka mwana wamwamuna. Iye anamupatsa dzina lakuti Samueli kutanthauza "wopempha kwa Mulungu". Hana sanayiwale kuti mwana wake Samueli anali yankho la pemphero lake. ***(1 Samueli 1: 19-20)*** *Nthawi zonse tikuyenera kumakumbukira kuyamika Mulungu akayankha mapemphero athu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Hana apemphera kwa Mulungu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***"Pemphani, ndipo chidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo chidzatsegulidwa kwa inu." (Mateyu 7:7)*** Fotokozani kuti mawu awa anayankhula ndi Yesu. Iye akufuna kutidalitsa. Kuposera zonse, Iye akufuna kutipatsa ife mphatso ya chipulumutso potipulumutsa ku machimo athu. |
| **KUMBUKIRANI** | Gwirtsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:<br>• Kodi Elikana ankapita kuti ndi banja lake chaka chilichonse?<br>• N'chifukwa chiyani Hana anali wokhumudwa?<br>• Kodi ndi chiyani chimene Hana sankafuna kuchita?<br>• Kodi Eli, wansembe, anaona chiyani pamene Hana ankapemphera?<br>• Kodi Hana analonjeza chiyani?<br>• Kodi Hana anamva bwanji mu mtima mwake atapemphera?<br>• Kodi mwana wakeyo anamupatsa dzina liti?<br>• Kodi dzina la mwana wake linkatanthauza chiyani? |

## C5 Nkhani Yachinayi

**Mulungu ayitana Samueli – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kuyankhula kwa ife.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Samueli anavomera pamene Mulungu anamuyitana.<br>• Aliyense pa yekha akuyenera kuyankha kuyitana kwa Ambuye.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 3: 9***<br>**Ndime Yowerenga:** ***1 Samueli 1: 21-3: 21*** |
| **MAWU OYAMBA** | Chitani sewero la "Kuyitana ndi Kuyankha" ndi ana. Mtsogoleri agwiritse ntchito ng'oma/kuwomba m'manja. Aziyimba ng'oma kapena kuwomba m'manja kanayi ndipo ana azitsanzira. Ana kumasintha pa utsogoleri. Pali masewero a "Kuyitana ndi Kuyankha" ambiri pogwiritsa ntchito mawu kapena zizindikiro. Chitsanzo, mtsogoleri ayitane kuti M.V.E. ndipo ana ayankhe kuti R.A.N.I! |
| **PHUNZITSANI** | • *Onaninso lonjezo limene anachita Hana mu phunziro la sabata yatha. Fotokozani kuti Samueli akanali wamng'ono, Hana anakwaniritsa lonjezo lake.* Anatenga Samueli ndi kupita naye ku Silo. Kumenekonso Hana anakapemphera kwa Mulungu. Nthawi iyi linali pemphero la chimwemwe chifukwa cha chimene Mulungu anali kwa iye. ***(1 Samuel 1: 24-2: 11)***<br>• Samueli ali wamng'ono anayamba kutumikira Mulungu. *Fotokozani kuti Samueli anali mwana wapadera kwambiri wokhalanso ndi ntchito ya padera. Mulungu anali ndi cholinga ndi moyo wa Samueli. Hana sanayiwale za Samueli.* Chaka chilichonse ankapita kukamuona ndi banja lake ndipo ankamubweretsera mkanjo watsopano. *Yankhulani za chisangalalo cha aliyense kuti chinali chotani nthawi imeneyi.* Pamene Samueli ankakula, moyo wake unkakondweretsa Mulungu ndipo ena amene ankamudziwa. *Yankhulani kwa ana amene mukuwaphunzitsa kuti mudziwe ngati miyoyo yawo ikukondweretsa Mulungu pamene akukula.* ***(1 Samueli 2: 18, 21, 26)***<br>• Usiku wina Samueli atapita kukagona, anamva wina akuyitana dzina lake. Samueli anaganiza kuti anali Eli, wansembe, ndipo anathamanga kupita kwa iye. Koma Eli anakana kuti sanamuyitane ndipo anamuwuza kuti apite akagone. *Fotokozani momwe izi zinkachitikira ndipo thandizani ana kuti aganize zomwe zinali m'maganizo a Samueli.* Pamene Samueli anamva kuyitana kwa dzina lake kachitatu, anathamanganso kupita kwa Eli, koma Eli nthawi iyi anazindikira amene ankamuyitana Samueli. Anali Mulungu. Eli anawuza Samueli kuti akamvanso akumuyitana, iye ayankhe kuti, "Yankhulani Yehova, pakuti mtumiki wanu ndikumvetsera." ***(1 Samueli 3: 1-9)***<br>• Atagona, Samueli anamvanso akumuyitana kachinayi. Samueli anayankha Yehova monga Eli anamuwuza. Mpaka nthawi imeneyi Samueli ankadziwa Yehova koma osati yekha ngati munthu. Samueli atadziwa kuti Mulungu akumuyitana, anayankha moyenera. *Lembani mzere mbali ya mawu oyamba a sewero.* Usiku umenewo Mulungu anamupatsa Samueli uthenga wofunika wa Eli. Unali uthenga woyamba mwa mauthenga ambiri amene Samueli analandira monga mneneri wa Mulungu. ***(1 Samueli 3: 10-21)***<br>• Mulungu ankadziwa dzina la Samueli. Iye amadziwa mayina athu tonse ndi amayitana aliyense pa yekha kuti alandire Mwana wake kukhala Ambuye ndi Mpulumutsi. *Fotokozani kuti kuyitana kwa Mulungu kwa ife sikumveka ngati mawu koma kudzera mwa Mzimu Woyera amene amatithandiza kuti tidziwe zomwe Mulungu akufuna kuti tichite. Mulungu amayankhula ndi ife pamene tikuwerenga Baibulo. Limbikitsani ana kuti adziwe kufunika koyankha moyenera.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI Zoonjezera C – Mulungu ayitana Samueli. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***1 Samueli 3: 9.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Gwiritsani ntchito mafunso awa monga njira yowakumbutsa nkhani:<br>• Kodi Hana anamutumiza Samueli kuti akagwire ntchito kuti?<br>• Kodi ankabweretsera chiyani chaka chilichonse?<br>• Kodi moyo wa Samueli unkakondweretsa ndani?<br>• Kodi ndani ankagwira ntchito ndi Samueli?<br>• Kodi Mulungu anamuyitana kangati Samueli?<br>• Kodi Samueli ankayenera kuyankha motani akamva Yehova akuyitana?<br>• Kodi Mulungu amadziwa mayina athu?<br>• Kodi tichite chiyani pamene Mulungu akutiyitana? |

## C6 Nkhani Yoyamba

**Kusankha mfumu – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kuyang'ana mu mtima.**

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Mulungu anawuza Samueli kuti asankhe Davide kukhala mfumu ya Israyeli.
- Mulungu amakondwera ndi chomwe ife tili – osati mmene tikuonekera.

**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 16: 7***
**Ndime Yowerenga:** ***1 Samueli 16: 1-13***

### MAWU OYAMBA

(Mu nkhani zinayi zotsatirazi muli zinthu zomwe talemba ndi zilembo **zowala** kuti muzionetse mukazitchula. Zimenezi mudzazigwiritsa ntchito pobwereza phunziro mu Nkhani Yachinayi.) Tiyerekeze kuti mwatumidwa kuti mukasankhe mfumu yatsopano, kodi inu mungasankhe munthu wotani? Ikani mayankho a ana m'magulu awiri – onena za maonekedwe ndi zomuyenereza. Kambiranani kuti zofunika kwambiri ndi ziti. N'kovuta kudziwa chomwe munthu ali ngati simunakumane naye n'kale lomwe. Monga chitsanzo, kutirani mphatso ziwiri, zonse zioneke bwino kunja kwake. Sankhani ana awiri kuti atsekule kuti aone yomwe ili yeniyeni ndi ina ya chinyengo.

### PHUNZITSANI

- Mulungu anatumiza Samueli pa ulendo wa mseri kuti akasankhe mfumu ya Israyeli. Samueli anasankhidwa ndi Mulungu kukhala mneneri kuti aziwuza anthu zimene Mulungu akunena kwa iwo. Mulungu sanakondwere ndi mfumu yoyamba ya Israyeli, Sauli, pakuti sinamvere Mulungu. ***(1 Samueli 15: 11)*** Samueli anakhumudwa ndi Sauli koma Mulungu anamuwuza kuti asakhumudwe. M'malo mwake, iye atenge botolo la mafuta a olivi **(onetsani)** ndi kupita kwa Jese wa ku Betelehemu amene anali ndi ana aamuna asanu ndi atatu. Werengani zomwe Mulungu anayankhula kwa Samueli. ***(1 Samueli 16: 1)***
- Samueli anali ndi nkhawa. Ngati Mfumu Sauli adzamva kuti munthu wina wasankhidwa kukhala mfumu, adzakwiya kwambiri ndipo adzayesetsa kuti amuphe Samueli. Mulungu anawuza Samueli kuti akapite, Jese ndi ana ake aamuna akakhale ndi mwambo wachipembedzo asanasankhe mfumu yatsopano. Samueli anamvera. *Ngati timakonda Mulungu, tikuyenera kumumvera ndi kuchita zimene Iye amanena m'Baibulo.* ***(1 Samueli 16: 2-3)***
- Samueli atafika ku Betelehemu, atsogoleri a mzindawo anali ndi mantha ndipo anafunsa ngati anabweretsa nkhani yoyipa. Samueli anafotokoza kuti anabwera kudzapembedza Mulungu ndi Jese ndi ana ake. Iye sanawawuze kuti anabwera kudzasankha mfumu yatsopano. *Chifukwa chiyani?* ***(1 Samueli 16: 4-5)***
- *Fotokozani zomwe zinachitika mu* ***1 Samueli 16: 6-11****, tsindikani zimene Mulungu anawuza Samueli pa* ***vesi 7****. Mulungu sakopeka ndi mmene munthu akuonekera kunja. Mulungu amafuna chomwe munthu ali. Iye amadziwa zomwe timaganiza za Iye ndi za anthu ena amene atizungulira. Onaninso chitsanzo chimene tinagwiritsa ntchito poyamba paja.*
- Davide anali mnyamata wathanzi amene nthawi zambiri ankakhala ku busa kuweta nkhosa za abambo ake **(onetsani)**. Gwiritsani ntchito *mawu a Mulungu kwa Samueli a pa* ***vesi 12b***. Samueli anakhuthulira mafuta a olivi pa mutu wa Davide monga chizindikiro kuti iye tsiku lina adzakhala mfumu! Mulungu anakhala ndi Davide kuyambira tsiku limenelo. Mulungu ankadziwa chimene chinali mu mtima wa Davide. Ngakhale anali wamng'ono kwambiri pakati pa ana a Jese, iye anasankhidwa monga munthu woyenera kukhala mfumu mu Israyeli. *Fotokozani kuti Mulungu amadziwa chimene aliyense wa ife ali. Mulungu sayang'ana msinkhu wathu, tsitsi lathu kapena maonekedwe athu abwino. Iye amayang'ana ngati timakonda Iye ndi Mwana wake, Ambuye Yesu.* ***(1 Samueli 16: 12-13)***

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**
**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kusankha mfumu.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***1 Samueli 16: 7***. Sankhani gawo lomaliza la vesiyi kuphunzitsa ana aang'ono.

### KUMBUKIRANI

Sakanizani zipangizo izi. Ana aziyikenso moyenera ndi pofotokozanso nkhaniyi.
Yankhulani pamodzi Vesi Yoloweza kapena yankhani mafunso:

- Kodi ndi ndani anali mfumu yoyamba ya Israyeli?
- Mulungu anasankha ndani kuti akapeze mfumu yatsopano?
- Kodi iye anapita kuti?
- Kodi iye popita anatenga chiyani?
- N'chifukwa chiyani Samueli anali ndi nkhawa?
- Kodi Samueli anawuzidwa kuti akapeze ndani ku Betelehemu?
- Kodi Jese anali ndi ana aamuna angati?
- Kodi mwana womaliza anabwera kwa Samuele anali ndani?
- Kodi Samueli anachita chiyani kusonyeza kuti Davide ndiye adzakhale mfumu yatsopano tsiku lina?
- Kodi Mulungu amakondweretsedwa ndi chiyani pa ife?

## C6 Nkhani Yachiwiri

**Kumenyana ndi Goliati – Iyi ndi nkhani ya Davide kudalira mphamvu ya Mulungu.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Davide ankadziwa kuti Mulungu adzamupatsa chipambano.
- Titha kukhala ndi chitsimikizo chachikulu mwa Mulungu wamoyo.

**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 17: 26***
**Ndime Yowerenga:** ***1 Samueli 17: 1-31***

**MAWU OYAMBA**

Kodi inu munachitapo mpikisano – woyenda/kusambira/kukhala chete woti mupeze ndalama za sukulu yanu kapena bungwe la zachifundo? *Kambiranani.* Mu nkhani ya lero gulu la ankhondo la Aisrayeli linakumana ndi vuto lalikuli - chiphona.
Dulani pepala la mamita atatu pa mpukutu ndi kuyala pansi. Ana ayambe kudziyeza okha ndi chimenechi - uwu ndiye unali msinkhu wa Goliati.

**PHUNZITSANI**

- Israyeli ndi Mfumu Sauli anali pa nkhondo ndi Afilisti. *Kumbutsani za kuti Aisrayeli anali anthu apadera a Mulungu ndipo nthawi zambiri m'mbuyomo ankawathandiza kupambana pa nkhondo akadalira Mulungu. Fotokozani zomwe zikuchitika apa, kuti gulu la ankhondo la Aisrayeli lili mbali ina ndipo Afilisti ali mbali inanso ndi pakati pawo pali chigwa.* Afilisti sankakonda kapena kudalira Mulungu. M'malo mwa magulu onse ankhondo kumenyana, Afilisti anatumiza msilikali wawo wamphamvu kwambiri, Goliati, kuti amenyane ndi gulu la ankhondo la Israyeli. Tsiku lililonse iye ankafuula kuti, "Sankhani munthu woti adzamenyane ndi ine." *Fotokozani za maonekedwe a Goliati ndi zida zake za nkhondo.* ***(1 Samueli 17: 4b-7)*** Mfumu Sauli ndi asilikali ake anali ndi mantha aakulu. Palibe ankalimba mtima kukamenyana ndi Goliati. ***(1 Samueli 17: 1-11)*** *Kodi mukuganiza kuti asilikaliwo akanachita chiyani?*
- Akulu ake atatu a Davide anali nawo m'gulu la ankhondo la Israyeli. *Kumbutsanani mayina awo ndi chifukwa chomwe ana aamuna atatuwa a Jese sanasankhidwe ndi Mulungu kukhala mfumu ya Israyeli.* Davide akudikira tsiku limene adzakhale mfumu, anapita ku busa kukasamalira nkhosa za abambo ake. Tsiku lina, Jese anawuza Davide kuti atenge chakudya **(onetsani buledi ndi majalini)** ndi kupita nacho kwa abale ake ku nkhondo. Davide anafika nthawi imene asilikali ankakhala pa mzere kukonzekera kuchita nkhondo ndipo anamva Goliati akuyankhula kuti akufuna munthu woti amenyane naye. Ankhondo a Israyeli anathawa chifukwa cha mantha. Mfumu Sauli inalonjeza mphotho yayikulu kwa munthu amene amenyana ndi Goliati ndi kumugonjetsa! ***(1 Samueli 17: 12-25)*** *Funsani ana aganize zomwe Davide ankamva mu mtima mwake pa nkhani imeneyi.*
- Davide anakwiya chifukwa Goliati ankanyoza ankhondo a Israyeli. Iye anati, "Mfilisti wosachita mdulidweyu ndi ndani kuti azinyoza gulu lankhondo la Mulungu wamoyo?" Davide anakwiya chifukwa panalibe ndi m'modzi yemwe akanatha kumenyana ndi chiphonachi. Iye ankadziwa kuti Mulungu adzawapatsa chipambano ndipo adzatha kupha Goliati. *Fotokozani zomwe Eliyabu anachita pa* ***vesi 28****.* Mfumu Sauli itamva zimene anayankhula Davide, inamuyitanitsa. ***(1 Samueli 17: 26-31)***
- *Mulungu analonjeza kusamalira anthu ake, Aisrayeli, ngati angadalire Iye. Afilisti ankapembedza milungu yopangidwa ndi mitengo ndi miyala koma Davide ankadalira Mulungu wamoyo. Iye ankadziwa kuti Mulungu adzapereka chipambano kwa munthu amene adzapita kukamenyana ndi Goliati. Ngati timakonda Mulungu wamoyo, ndiye kuti Iye ali mbali yathu, kutiyang'anira.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**
**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kumenyana ndi Goliati.

**PHUNZIRANI**

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***1 Samueli 17: 26***. Khazikikani gawo lomaliza la vesiyi. Fotokozani kuti anthu wosadulidwa anali anthu amene si Ayuda ndipo ankapembedza milungu yopangidwa ndi anthu osati Mulungu wamoyo.

**KUMBUKIRANI**

Funsani ana ajambule chithunzi cha zida za Goliati pa pepala lomwe tinagwiritsa ntchito poyamba lija ndipo alembe zomwe anayankhula Goliati kwa gulu la ankhondo la Israyeli. Kapena gwiritsani ntchito mafunso awa:
- Ndi ankhondo ati amene ankamenyana ndi Mfumu Sauli ndi Aisrayeli?
- Kodi chiphona chawo dzina lake anali ndani?
- Kodi msinkhu wake unali wautali motani?
- Tchulani zida za nkhondo zomwe anali nazo.
- Kodi iye ankayankhula mawu otani kwa gulu la ankhondo la Israyeli?
- Kodi Davide ankachita chiyani pamene abale ake anali ku nkhondo?
- Kodi abambo ake anamutuma kuti akachite chiyani?
- Kodi Davide anamva chiyani atangofika ku msasa wa ankhondo?
- Kodi chinakwiyitsa Davide ndi chiyani?
- Kodi ndani anayitanitsa Davide?

## C6 Nkhani Yachitatu
**Kugonjetsa Goliati – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kupereka chipambano.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Mulungu anamupatsa Davide kulimba mtima ndi chipambano pa Goliati.
- Mulungu amapereka chipambano kwa amene amamukonda ndi kumudalira.

**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 17: 47***
**Ndime Yowerenga:** ***1 Samueli 17: 32-51***

### MAWU OYAMBA

Onaninso C6, Nkhani Yachiwiri, kuchokera pa zithunzi za FBI.
Funsani ana zinthu zimene amachita nazo mantha. Davide sankachita mantha kumenyana ndi Goliati chifukwa ankadziwa kuti Mulungu anali naye.

### PHUNZITSANI

- Davide anayima pamaso pa Mfumu Sauli. Fotokozani zomwe anakambirana mu ***vesi 32-33***. Davide ankadziwa kuti panalibe chifukwa chochita mantha ndi Goliati chifukwa Mulungu anali mbali ya gulu la ankhondo a Israyeli. Koma Davide anazolowera kukumana ndi zoopsa. Pamene ankaweta nkhosa za abambo ake, anapha mkango ndi chimbalangondo mothandizidwa ndi Mulungu. Kaya ndinu wamng'ono, Mulungu angathe kukuthandizani kuchita zinthu zofunika. *Fotokozani zimene Davide akuyankhula mu* ***vesi 34-37***. Davide anali ndi chitsimikizo kuti Mulungu adzamupulumutsa kuti asaphedwe ndi Goliati. ***(1 Samueli 17: 32-37)***
- Mfumu Sauli inavomereza kuti Davide apite akamenyane ndi Goliati. *Lolani ana aganizire Davide atavala zida za Sauli ndipo akulephera kuyenda nazo chifukwa cha kulemera.* Davide anawuza mfumu kuti sakanatha kumenya nkhondo atavala zida zimenezo ndipo anavula. *Fotokozani zomwe anachita mu* ***vesi 40****. Onetsani miyala yabwino isanu ili m'thumba.* ***(1 Samueli 17: 38-40)***
- *Fotokozani mmene Goliati ankayendera ndi kumaseka pamene ankapita kunali Davide kamnyamatako kopanda zida koma katanyamula legeni.* Davide sankachita mantha. Iye ankadziwa kuti anali ndi Mulungu. Iye anawuza Goliati kuti, "Ine ndikubwera kwa iwe m'dzina la Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa ankhondo Aisrayeli." *Onaninso za kuti Afilisti sankapembedza Mulungu wamoyo, koma milungu ya mitengo ndi miyala. Fotokozani mwachidule zimene Davide ananena mu* ***vesi 46-47***. Davide anafotokoza momveka bwino kuti sizinali mphamvu zake, koma mphamvu ya Mulungu imene idzagonjetsa Goliati. Iye ankadziwa kuti Mulungu anali mbali yake. ***(1 Samueli 17: 41-47)***
- Nthawi yomweyo, Davide anapitsa dzanja lake m'thumba muja *(fanizirani)*, ndipo anatenga mwala ndi kuwuyika pa legeni. Iye anapukusa legeni ndi kuponya mwalawo ndipo unakamenya pakati pa chipumi cha chiphonacho **(onetsani)**. Munthu wotalika mamita atatu anagwa pansi. Davide anagwiritsa ntchito **lupanga** la Goliati kumuphera. Pamene Afilisti anaona kuti Goliati wafa anathawa. Mulungu anali atapereka chipambano kwa Davide ndi Aisrayeli. *Uzani ana ayamikire mofuula!* ***(1 Samueli 17: 48-51)***
- Davide anadalira Mulungu kuti adzamupatsa chipambano. *Fotokozani kuti ife lero sitimenyana ndi ziphona. Mdani wathu ndi Satana kapena mdierekezi amene amafuna kuti ife tizichita zolakwa. Ife tiyenera kumenya nkhondo yogonjetsa zoyipa m'miyoyo yathu. Ngati timakonda Mulungu ndipo tinamupempha kuti atikhululukire tchimo lathu, ndiye Iye ali mbali yathu. Ngati timupempha Mulungu, Iye adzatithandiza kuti tisachite zolakwa ndi kukhala moyo wokondweretsa Iye.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**
**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kugonjetsa Goliati.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***1 Samueli 17: 47***. *Fotokozani kuti mawu awa anayankhula ndi Davide kwa Goliati.*

### KUMBUKIRANI

- N'chifukwa chiyani Mfumu Sauli inkaganiza kuti Davide sanali woyenera kumenyana ndi Goliati?
- Kodi ndi zida ziti za Sauli zimene anamupatsa Davide?
- Kodi m'malo mwake Davide anagwiritsa ntchito chiyani?
- Kodi Davide ananena chiyani kwa Goliati atakumana?
- Kodi Davide anagwiritsa ntchito miyala ingati kuti Goliati agwe pansi?
- Kodi gulu la ankhondo a Afilisti linachita chiyani litaona kuti Goliati wafa?
- Kodi ndi mphamvu ya ndani imene inagonjetsa Goliati?
- Kodi 'mdani' wathu ndi ndani?
- Kodi ndi ndani adzatipatsa chipambano ndi kutithandiza kuti tisachite zinthu zoyipa?

## C6 Nkhani Yachinayi

**Kukhala ndi Sauli – Iyi ndi nkhani ya chitetezo cha Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>• Nsanje inachititsa kuti Mfumu Sauli idane ndi Davide.<br>• Mulungu anateteza Davide pamaso pa Mfumu Sauli.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 18: 14***<br>**Ndime Yowerenga:** ***1 Samueli 18: 1-16*** |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana kuti apereke zitsanzo za nsanje. Fotokozani kuti munthu atha kukhala ndi nsanje chifukwa cha zimene wina akuchita - monga, kuchita nsanje ndi munthu wanzeru kapena waluso la masewera. Kapena nsanje itha kubwera chifukwa wina ali ndi chinthu chimene iwe ulibe – monga, zovala zabwino. Baibulo limatiphunzitsa kuti nsanje ndi yoyipa ndipo itha kutichititsa zoyipa ngati tingayilole kukula mwa ife. Mulungu anatilenga anthu osiyanasiyana, choncho tikuyenera kuyamikira chimene anatipatsa m'malo mochitira nsanje ena. (Onani nsanje mu C1 Nkhani Yachitatu.) |
| **PHUNZITSANI** | • Davide anali ngwazi! Iye atapha Goliati, chiphona chija, Mfumu Sauli inakondwera naye ndipo inamutenga ndi kumakakhala naye ku nyumba yaufumu. Davide ndi mwana wa mfumu, Jonatani, anakhala abwenzi. Iwo analonjezana kuti adzakhala abwenzi moyo wawo wonse. Jonatani anamupatsa Davide mphatso **(lembeni mphatsozo ndipo onetsani mkanjo ndi lamba)** kufuna kuonetsa ubale wawo kuti unali wamphamvu. *Yankhulani za abwenzi a pamtima a ana.* Ndi chabwino kukhala ndi abwenzi amene amakhalabe abwenzi posatengera zomwe zachitika.<br>• Davide anasanduka munthu wofunika kwambiri mu gulu la ankhondo la Mfumu Sauli. Chilichonse chimene Sauli ankamupatsa kuti achite, ankachichita bwino kwambiri. Asilikali anzake ndi anthu a Israyeli ankakondwera naye. Atapha Goliati, Davide ndi Mfumu Sauli anabwerera ku Yerusalemu. Amayi anabwera m'misewu ndi zoyimbira zawo **(onetsani***, ngati n'kotheka)*. Awuzeni ana nyimbo imene ankayimba akuvina. ***(1 Samueli 18: 5-7)***<br>• Kodi mukuganiza kuti ndi ndani anakwiya ataona zimenezi? *(Mfumu Sauli)* Iye anachitira nsanje Davide, mpaka ankafuna kumupha. *Mkwiyo ndi nsanje zimachititsa anthu kuganiza ndi kuchita zinthu zoyipa. Mulungu anachenjeza za kuchitira nsanje anthu ena.* ***(Eksodo 20: 17)*** Mfumu Sauli inafunafuna mpata woti aphe Davide. Tsiku lililonse, Davide ankayimba zeze mu nyumba yaufumu kufuna kutonthoza Mfumu Sauli ndipo zinkathandiza kuti afatse kapena kukhala wosakwiya. Koma fotokozani zomwe zinachitika tsiku lotsatira pamene Sauli anafuna kupha Davide kawiri. Sauli ankachita mantha ndi Davide chifukwa ankaona kuti Mulungu ankamusamalira. Iye anaona molondola zonse za Davide koma osati za iye mwini. ***(1 Samueli 18: 8-12)***<br>• Mfumu Sauli inatumiza Davide ku nkhondo ndi asilikali 1,000. Iye ankaganiza kuti Davide akaphedwa ku nkhondo. ***(1 Samueli 18: 17b)*** Koma Mulungu anateteza Davide ndi Mulungu anamupambanitsa pa chilichonse chimene ankachita. Mfumu Sauli inakhala ndi nsanje yayikulu ndiponso mantha. Koma anthu ankakonda Davide chifukwa anali mtsogoleri wa asilikali wabwino. ***(1 Samueli 18: 13-16)***<br>• Davide ankakonda Mulungu, ndipo Mulungu ankamuteteza ku zoyipa. Tsiku lina adzakhala mfumu ya Israyeli. *Ngati tikonda Mulungu ndi kufuna kumvera zimene Iye akunena m'Baibulo, pamenepo Mulungu adzatiyang'anira ndi kutisamalira.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukhala ndi Sauli. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***1 Samueli 18: 14.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Tengani zinthu zonse zimene mwagwiritsa ntchito pophunzitsa C6 (chidole cha nkhosa, mafuta a olivi, buledi ndi majalini, miyala isanu m'thumba, chidole cha lupanga, mkanjo, lamba ndi choyimbira). Bwerezani kufotokoza chifukwa chomwe izi zili mu nkhaniyi ndipo kenaka ana aziyike mu ndondomeko yoyenera ndi nkhaniyi.<br>Kalasi 1, ana amasangalala akamasewera seweroli - ikani zonse ndipo chotsani china wina aliyense asakuona. Kodi mungadziwe chimene chasowa pamenepo? |

# Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

**Maphunziro a Kalasi Yoyamba**
- Sabata lililonse pali masamba anayi amene akufunika kuchekenira ndi kulembamo mawu pang'ono.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 amene akuyenera kuperekedwa kuchokera pa marikisi 80 a mwezi onse.
- Ana amene akuphunzira maphunziro a Kalasi Yoyamba iwo sakuyenera kuwerenga chifukwa sangathe kuwerenga bwino ndipo tikuyembekezera makolo/owang'anira/atsogoleri awo kuwathandiza.

**Maphunziro a Kalasi Yachiwiri**
- M'buku muli maphunziro anayi pa sabata.
- M'phunziro lililonse muli nkhani. Ophunzira akuyenera kupeza mawu osiyanasiyana m'phunziro, ndi kuchekenira, kutsiriza Mavesi Oloweza ndi zina zambiri.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 pa marikisi 80 a mwezi uliwonse pamene atsiriza maphunziro onse molondola.

**FUNDO ZA KACHONGEDWE**

Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:
- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolembera, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitso kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.

Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

**Kalasi Yoyamba**
**Ndemanga zina**
"Chikondi – Ine ndasangalala kuti inu mwayamba maphunziro awa ndipo ndikukhulupirira kuti muwakonda. Zochekenira zanu ndazikonda. Kodi mumapita ku sukulu? Ndikuyembekezera kumva kuchokera kwa inu posachedwa."
"Wachita bwino, Andreya. Wachekenira bwino kwambiri! Kodi zimavuta pamene mumachekenira mizere ya m'kati? Inu musiyako zochepa zokha munachekenira pang'ono phunziro lapita lija."

**Ndemanga zauzimu**
"Wachita bwino, Sarah. Yairo analitu munthu wokondwa kwambiri pamene Yesu anamuthandiza."
"Yankho labwino kwambiri! Nkhani ya kufa kwa Yesu ndi yomvetsa chisoni, koma chokondweretsa ndi chakuti Iye anaukanso."

**Kalasi Yachiwiri**
**Ndemanga zina**
"Yankho labwino, Chimwemwe – Ine ndikukhulupirira kuti aphunzitsi ako akusangalala kwambiri ndi ntchito yako ku sukulu!"
"Ine ndikudziwa kuti posachedwapa ndi tsiku lako lobadwa, Chisomo. Kodi udzachita phwando? Udzachitira kuti? Udzakhale ndi tsiku lopambana kwambiri!"
"Iwe wayesetsa kwambiri. Pali zolakwika zochepa chabe. Usamayiwale kuonanso mayankho nthawi iliyonse."

**Ndemanga zauzimu**
"Ine ndasangalala ndi mmene wachekenira chithunzi cha Yesu ali nkhanda modyera ng'ombe. Kodi sizinali zabwino kuti Mulungu atumize Mwana wake ku dziko lapansi kwa ife?"
"Mitundu yako ndayikonda kwambiri! Zakariya anapereka dipo chifukwa cha kusakhulupirira zimene Mulungu ananena. Iye anakayikiranso Mawu a Mulungu."
"Mayankho abwino kwambiri. Munthu amene anakumana ndi Filipo ku chipululu anapita kwawo akusangalala kwambiri. Iye anamva ndi kukhulupirira nkhani yabwino ya Yesu."

## Zoonjezera A - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| C1 | Danieli | **Dziko lachilendo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-daniel/ (slides 1 & 2) |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-daniel/ |
| | | **Fano la Nebukadinezara** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/fiery-furnace-preschool/ |
| | | **Zenera lotsekula** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/daniel-lions-preschool/ |
| | | **Dzenje la mikango** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-daniel/ |
| | | |
| C2 | Zodabwitsa Zina Zambiri | **Munthu wosaona aona** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-blind-man/ |
| | | **Kudyetsa gulu la anthu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-5000/ |
| | | **Munthu wolumala ayenda** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-jesus-bethesda/ |
| | | **Mtsikana womwalira akhala moyo!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jairus/ |

## Zoonjezera A - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| C1 | Danieli | **Dziko lachilendo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/daniel-food/ |
| | | **Ng'anjo yamoto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/meshach-shadrach-abednego/ |
| | | **Zenera lotsekula** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-daniel/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-daniel/ |
| | | **Dzenje la mikango** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-daniel/ |
| | | |
| C2 | Zodabwitsa Zina Zambiri | **Munthu wosaona aona** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-blind-man/ |
| | | **Kudyetsa gulu la anthu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-boy-lunch/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-feeding-5000/ |
| | | **Munthu wolumala ayenda** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-jesus-bethesda/ |
| | | **Mtsikana womwalira akhala moyo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-jairus/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jairus-daughter/ |

| Zoonjezera B - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **C3** | **Anthu Amene Yesu** | **Zakeyu** |
| | **Anakumana Nawo** | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-zacchaeus-preschool/ |
| | | **Nikodemo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-nicodemus/ |
| | | **Mayi wa ku Samariya** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-018-samaritan-woman/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-019-living-water/ |
| | | **Mnyamata wachuma** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-074-rich-ruler/ |
| | | |
| **C4** | **Imfa ya Khristu** | **Yudase** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-jesus-passover-1/ |
| | | **Pilato** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-trial/ |
| | | **Yosefe** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-dies/ |
| | | **Anthu awiri a paulendo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-emmaus/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-alive/ |

| Zoonjezera B - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **C3** | **Anthu Amene Yesu** | **Zakeyu** |
| | **Anakumana Nawo** | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-zacchaeus/ |
| | | **Nikodemo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-017-nicodemus/ |
| | | **Mayi wa ku Samariya** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-samaritan-woman/ |
| | | **Mnyamata wachuma** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-rich-man/ |
| | | |
| **C4** | **Imfa ya Khristu** | **Yudase** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-085-judas-betrays/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-089-prayer-garden/ |
| | | **Pilato** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-092-jesus-pilate/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-093-mocking-jesus/ |
| | | **Yosefe** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-099-jesus-burial/ |
| | | **Anthu awiri a paulendo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-103-appearance-emmaus/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/disciples-emmaus/ |

## Zoonjezera C - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| C5 | Rute ndi Samueli | **Rute** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-1/ |
| | | **Rute ndi Boazi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-1/ |
| | | **Hana apemphera kwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-2/ |
| | | **Mulungu ayitana Samueli** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-3/ |
| | | |
| C6 | Davide | **Kusankha mfumu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-david/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/fn-samuel-david/ |
| | | **Kumenyana ndi Goliati** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-david/ |
| | | **Kugonjetsa Goliati** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-david/ |
| | | **Kukhala ndi Sauli** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-david-saul/ |

## Zoonjezera C - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| C5 | Rute ndi Samueli | **Rute** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-1/ |
| | | **Rute ndi Boazi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-2/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-3/ |
| | | **Hana apemphera kwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-samuel-saul/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-born/ |
| | | **Mulungu ayitana Samueli** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-3/ |
| | | |
| C6 | Davide | **Kusankha Mfumu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-david-goliath/ |
| | | **Kumenyana ndi Goliati** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-david-goliath/ |
| | | **Kugonjetsa Goliati** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-david-goliath/ |
| | | **Kukhala ndi Sauli** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-jonathan/ |

© Bible Educational Services 2023

www.besweb.com

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 12/2024
(Chichewa)